
# Mau a masiku onse

## Mau a masiku onse ocokera m’Baibulo




Mau anu ndiwo nyali ya ku mapazi anga – Salimo 119.105






# Cilengedwe ca Mulungu

## Paciyambi Mulungu adalenga Kumwamba ndi dziko lapansi – Genesis 1.1






**1 January – Mulungu analenga kuunika**

<u>Werengani Genesis 1.1-5</u>

M'mutu woyamba wa Baibulo tiwerenga kuti Mulungu analenga zonse. Asanalenge ciriconse kunalibe kalikonse koma Mulungu yekha. Mulungu analiko nthawi zonse ndipo adzakhalako nthawi zonse. Iye ndiye wamuyaya. Mulungu sanagwiritse nchito ciriconse kuti alenge. Analankhula mau ndipo kunacitika. Anati, 'Kuyere'. Ndipo kunayera. Mulungu akwaniritsa kucita kalikonse komwe afuna.

**Funso: Kodi kutanthauza ciani kwa inu kuti Mulungu akhalako nthawi zonse?**







## 2 January – Thambo

Werengani Genesis 1.6-8

Pa tsiku laciwiri Mulungu analenga thambo. Kumwamba kwa thambo kuli Kumwamba kumene Mulungu akhala. Munthu aliyense amene ali mwana wake adzakhala naye Kumwamba ku nthawi zonse.

## 3 January – Dziko, nyanja, zomera ndi mitengo

Werengani Genesis 1.9-13

Mulungu anapanga malo kuti madzi akhaleko: nyanja, mitsinje ndi dziwe. Pambuyo pake mtunda unaoneka. Mulungu anaucha mtunda dziko lapansi. Analenganso zomera ndi mitengo.

## 4 January – Dzuwa, mwezi ndi nyenyezi

Werengani Genesis 1.14-19

Dzuwa limene tiona linalengedwa ndi Mulungu. Mwezi ndi nyenyezi zinalengedwanso ndi Iye. Baibulo likamba kuti Mulungu ali monga dzuwa. Mulungu ndi wabwino kwambiri.

## 5 January – Nyama

Werengani Genesis 1.20-23

Pa tsiku lacisanu Mulungu analenga nyama zonse zimene zimakhala mumlengalenga ndi m'madzi. Zonse zimene Mulungu analenga zioneka bwino kwambiri.

## 6 January – Nyama zina ndi anthu

Werengani Genesis 1.24-31

Pa tsiku lacisanu ndi cimodzi Mulungu analenga nyama zina zonse. Analenganso Adamu: munthu woyamba. Mulungu anagwiritsa nchito nthiti ya Adamu kupanga Hava. Zonse zinali m'mgwirizano wabwino: Mulungu, anthu ndi cilengedwe cina.


## 7 January – Mulungu anamariza

Werengani Genesis 2.1-3

Pa tsiku lacisanu ndi ciwiri Mulungu sanalenge ciriconse. Anakondwera ndi cilengedwe cake coyenerera. Sabata lirilonse Mulungu atipatsa tsiku limodzi kuti tipezenso nthawi yomtamandira ndi kulemekeza Iye. Tsiko ilo ndi tsiku la Sabata.

# Adamu ndi Hava m'Paradaiso

Pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu
Aroma 3.22



**8 January – Kucokera ku nthawi ya kulenga**

Werengani Genesis 3.1-5

Cilengedwe ca Mulungu cinali cabwino. Mulungu, Adamu ndi Hava ndi nyama zonse zinasangalala. Anakondwera kukhala pamodzi. Munali mitengo yambiri m'Paradaiso. Adamu ndi Hava anadyako. Sanaloledwe kudya mtengo umodzi. Mtengo uwo ndi mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa. Mulungu anauza Adamu ndi Hava kuti sadzakondwera atadya mtengo uwo. Sadzakhala ndi moyo, koma adzafa ndi kusiyanitsidwa ndi Mulungu. Mulungu sanafune kuti adzikhala osasangalala. Mulungu anawaletsa kudya mtengo uwo.

Koma Satana anafuna Adamu ndi Hava kukhala osasangalala. Satana ndi mdani wa Mulungu. Satana ananyenga Hava. Anati kuti anthu atadya mtengo adzakhala ngati Mulungu ndipo sadzafa. Satana afunabe kuononga zonse ndi kusakondweretsa anthu onse.

**Funso: Kodi mumamvera Mulungu kapena Satana? Kodi umoyo wanu uonetsa kuti mumamvera yani?**

**9 January – Kusamvera**

Werengani Genesis 3.6-8

Hava anaganiza kuti Satana adati coonadi. Anadyako mtengo. Adamu anacita cimodzi-modzi monga mkazi wake. Iwo awiri sanamvere Mulungu. Kusamvera ndiko kuukira Mulungu. Ndiko chimo. Mulungu akuda macimo.

**10 January – Mulungu anafuna Adamu ndi Hava**

Werengani Genesis 3.9-13

Mulungu anadziwa kuti Adamu ndi Hava sadamvere. Komabe anawafunafuna. Mulungu afuna anthu osamvera kubwerera kwa Iye ndi kulapa. Iye ndiye wacifundo.

**11 January – Mulungu analonjeza Yesu**

Werengani Genesis 1.14 and 15

Mulungu sanalole Satana kupambana. M'ndime ya 15 analonjeza kuti adzatuma Mwana wake Yesu Kristu. Yesu anadza kuti afe pa mtanda. Anagonjetsa Satana ndi macimo. Mulungu ndi wamphamvu kuposa Satana.

**12 January – Dziko ndi lotembereredwa**

Werengani Genesis 3.16-19

Dziko lonse lapansi ndi lotembereredwa cifukwa ca uchimo. Mabvuto omwe tikomana nao m'umoyo wathu ndiwo otsatira a chimo loyamba m'Paradaiso. Tsiku lina tidzafa.

**13 January – Kuthawitsidwa**

Werengani Genesis 3.20-24

Adamu ndi Hava anathawitsidwa m'Paradaiso ndipo sanakhoze kubwereranso. Anadziwa kuti adzafa. Tikhale ndi moyo wosatha mwa Yesu yekha.

**14 January – Njira yeniyeni yopulumutsidwemo**

Werengani Aroma 3.23 and 24

Anthu onse samvera Mulungu. Ndife ocimwa. Mulungu safuna ocimwa kukhala naye Kumwamba. Macimo anu ayenera kucotsedwa. Yesu akwaniritsa ndipo afuna kucotsa macimo anu.

# Baibulo ndilo Mau a Mulungu

Ndidzadzikondweretsa nao malemba anu; Sindidzaiwala mau anu – Salimo 119.16

**15 January – Uthenga wa Mulungu**

Werengani 2 Petro 1.20 and 21


M'umoyo wathu wa masiku onse tikonda kumva za banja lathu ndi anzathu. Tikonda kulandira uthenga. Baibulo ndinso uthenga: uthenga wocokera kwa Mulungu. Tikawerenga Baibulo Mulungu alankhula nafe.

M'Baibulo tiwerenga kuti Mulungu ndiye yani. Kuli Mulungu m'modzi. M'Mulungu muli atatu: Mulungu Atate, Mulungu Mwana (Yesu) ndi Mulungu Mzimu Woyera. Tikamba kuti ndi Utatu Woyera wa Mulungu.

Baibulo iri ndi zigawo ziwiri. Cigawo coyamba cinenedwa Cipangano Cakale. M'Cipangano Cakale tiwerenga zimene zinacitika asanabadwe Yesu. M'Cipangano Catsopano tiwerenga za kubadwa kwa Yesu ndi zimene zinacitika atabadwa Iye.

Mulungu anauza anthu osiyanasiyana kuti alembe mau ake, monga Mose, Yesaya, Luka ndi Paulo. Mabuku ena a m'Baibulo atiuza za umoyo wa anthu. Ena ndiwo nyimbo kapena makalata olembera Akristu (anthu amene ali a Yesu Kristu). Kuli zambiri zimene tingaphunzire!

**Funso: Kodi Baibulo litanthauza ciani kwa inu?**



**16 January – Nyali**

Werengani Salimo 119.105

Tikapita pabwalo usiku tifunika nyali. Kopanda nyali ndi koopsa. Baibulo ndilo monga nyali. Litiuza za Mulungu ndi uchimo. Litiuza za Yesu. Kukhala kopanda Baibulo ndi koopsa.

**17 January – Baibulo ndi lofunikira**

Werengani 2 Timoteo 3.16 and 17

Baibulo litiphunzitsa zonse zimene tiyenera kudziwa. Mukafuna kukhala Mkristu woona mufunika Baibulo.

**18 January – Yesu**

Werengani Yohane 5.39

Baibulo litithandiza kupeza Yesu. Tifunika kudziwa Yesu kuti tipulumuke ku macimo athu. Tikapeza Yesu tikhala ndi moyo wosatha. Pemphani Mulungu kuti akuthandizeni kumvetsetsa zimene Baibulo likamba.

**19 January – Citsogozo**

Werengani Salimo 119.9

Baibulo litiuza zimene ziri zabwino ndi zoipa. Sitikhoza kugamula mlandu pa zimene Mulungu akamba za zabwino ndi zoipa (Eksodo 20). Kodi mumacita zimene Baibulo likuphunzitsani?

**20 January – Kumbukirani mau a Mulungu**

Werengani Deuteronomo 11.18-21

Mulungu anafuna kuti Aisrayeli akumbukire zimene Iye akamba. Tiyeneranso kukumbukira zimene Mulungu akamba m'Baibulo. Kodi mungacite ciani kuti mukumbukire zimene Mulungu akamba m'Baibulo?

**21 January – Kugonjetsa Satana ndi uchimo**

Werengani Mateyu 4.1-11

Satana anafuna kucimwitsa Yesu. Yesu anakana kusamvera Mulungu. Yesu anagwiritsa nchito mau a Mulungu kugonjetsa Satana. Tikafuna kugonjetsa Satana ndi uchimo tifunika kudziwa zimene Baibulo likamba.

# Combo ca Nowa

Pakuti Yehova Mulungu ndiye dzuwa ndi cikopa; Yehova adzapatsa cifundo ndi ulemerero; Sadzakaniza cokoma iwo akuyenda angwiro – Salimo 84.11



**22 January – Zimene Mulungu anaona**

Werengani Genesis 6.5-10

Mulungu akhala Kumwamba, koma aona zimene zicitika pa dziko lapansi. Adziwa zimene ticita, tikamba ndi kuganiza.

Mulungu sanakondwere ataona ana a Adamu ndi Hava. Anthu anadzikonda m'malo mwa kuganizira Mulungu (Mateyu 24.38). Mulungu anakhumudwa. Anati kuti kudzakhala bwino ngati anthu onse afa. Ico ndi cilango cao.

Kunali munthu m'modzi yemwe anali mnzake wa Mulungu. Munthuyo ndi Nowa. Mulungu anafuna kupulumutsa Nowa ndi banja lake.

**Funso: Kodi Mulungu aona ciani pamene ayang'anira umoyo wanu?**

**23 January – Nowa anapanga combo**

Werengani Genesis 6.11-14

Mulungu anauza Nowa kupanga combo cacikulu. Banja la Nowa lidzakhala lotetezeka mkati mwa combo pamodzi ndi nyama zambiri. Nowa anacita zimene Mulungu anamuuza. Anacenjeza anthu ena kuti aleke kucimwa ndipo kuti alape, koma anamseka.

**24 January – Kucedwa kwambiri**

Werengani Genesis 7.11-16

Mvula yaikulu inalokwa. Nyama zinali zotetezeka m'combo pamodzi ndi banja la Nowa. Anthu ena anacedwa kulapa kuti apeze citetezo. Lapani ku macimo anu, musanacedwe kwambiri.

**25 January – Kopanda citetezo kubwalo**

Werengani Genesis 7.17-24

Onse omwe sanalowe m'combo anamizidwa m'madzi. Ico cinali cilango ca Mulungu. Tiyeneranso kulangidwa. Cifukwa ca macimo athu tiyenera kukhala ku Gehena pamene tidzafa. Gehena ndi malo oipa oposa kumene Satana akhala. Yesu yekha ndi Njira yopulumutsa.

**26 January – Kunaumanso**

Werengani Genesis 8.6-14

Madzi anacoka pang'ono-pang'ono. Patapita nthawi Nowa anatuma mbalame kuti adziwe ngati madzi onse adacoka. Tsiku lina anadziwa kuti madzi onse anacoka. Dziko lapansi linaumanso.

**27 January – Kutuluka m'combo**

Werengani Genesis 8.15-22

Cilango ca Mulungu cinapita. Mulungu anauza Nowa kutuluka m'combo ndi kuyamba moyo watsopano pa dziko lapansi. Nowa anamanga guwa la nsembe kuyamika Mulungu. Nowa anali woyamikira Mulungu pakuti Mulungu anamteteza.


**28 January – Utawaleza**

Werengani Genesis 9.8-16

Mulungu analonjeza Nowa kuti sadzaononganso dziko lapansi ndi madzi osefukira. Utawaleza ndi cizindikiro ca cilonjezo ca Mulungu. Tikaona utawaleza tikumbutsidwa ndi nthano ya Nowa ndi cifundo ca Mulungu.

# Umoyo wa Abrahamu

Ndi cikhulupiriro Abrahamu, poitanidwa, anamvera kuturuka kunka ku malo amene adzalandira ngati colowa – Ahebri 11.8a



**29 January – Mulungu anaitana Abramu**

<u>Werengani Genesis 12.1-5</u>

Mulungu anauza Abramu kusiya nyumba ya tate wake ndi kuturuka m'dziko lake. Abramu anayenera kudalira pa Mulungu yekha. Mulungu analonjeza Abramu kukhala ndi ana ambiri, ngakhale akalamba. Abramu anayenera kuphunzira kuti Mulungu acita zimene alonjeza. Abramu anamvera Mulungu. Anasiya zonse ndipo anayamba ulendo wake pamodzi ndi anthu ena ocepa. Anadza ku dziko locedwa Kanani.

**Funso: Kodi mumvera Mulungu m'njira yotani m'umoyo wanu?**

**30 January – Kuwerenga nyenyezi**

Werengani Genesis 15.1-5

Kunacitika zambiri atayamba Abramu ulendo wake. Analibe mwana. Anadera nkhawa. Mulungu anamuuza kuti mbeu yake idzakhala yambiri monga nyenyezi. Abramu anakhulupirira kuti adzakhaladi ndi mwana ngakhale kunaoneka kuti ndi kosatheka.

**31 January – Ganizo**

Werengani Genesis 16.1-4 and 16.15

Abramu ndi Sarai analibe mwana. Anafuna Abramu kulandira mwana wa mdzakazi wa Sarai. Dzina la mwana ndi Ismayeli. Zimene Abramu anacita zinapangitsa mabvuto ambiri. Aziyembekezera Mulungu. Kodi muyembekezera Mulungu?

**1 February – Lonjezo la Mulungu**

Werengani Genesis 18.1-15

Mulungu anacha Abramu Abrahamu ndi Sarai Sara. Anawatsimikiziranso kuti adzakhala ndi mwana. Patapita nthawi Mulungu anawayendera. Anawalonjezanso kuti adzakhala ndi mwana. Sara sanakhulupirire kuti ndi coonadi.

**2 February – Kubadwa kwa Isake**

Werengani Genesis 21.1-7

Patapita zaka zambiri Mulungu anacita zimene adalonjeza. Abrahamu ndi Sara analandira mwana. Anamucha Isake. Ndi cotheka kuti tiyenera kuyembekeza nthawi yaitali koma Mulungu amacita zimene akamba nthawi zonse.

**3 February – Ismayeli anacotsedwa**

Werengani Genesis 21.8-13

Ismayeli sanali wokoma mtima kwa Isake. Mulungu anafuna Abrahamu kucotsa Ismayeli ndi mai wake Hagara. Ismayeli sanali mwana wa malonjezano. Abrahamu anamvera Mulungu ngakhale sanafune kuwacotsa poyamba.

**4 February – Nsembe**

Werengani Genesis 22.1-14

Mulungu anayesa kumvera kwa Abrahamu. Mulungu anamupatsa nkhosa imene inafa m’malo mwa Isake. Ici citiphunzitsa za Yesu. Iye anafa pa mtanda kuti akhululukira macimo a anthu ake.

# Loti, mwana wa mphwace wa Abrahamu

Ndipo pakuisandutsa makara midzi ya Sodoma ndi Gomora anaitsutsa poigwetsa, ataiika citsanzo ca kwa iwo akakhala osapembedza

2 Petro 2.6



**5 February – Kusankha malo okhalako**

Werengani Genesis 13.5-13

Loti anali mwana wa mphwace wa Abrahamu. Iwo awiri anali ndi nyama zambiri. Malo anali ocepekera. Anaganiza za kusiyana. Loti anasankha malo obereka bwino. Ku malo komwe Loti anasankha kunakhala anthu oipa kwambiri. Abramu anapita ku malo obereka pang'ono.

**Funso: Kodi mungasanke malo obereka bwino kapena malo kumene anthu omvera Mulungu akhalako?**

**6 February – Kutengedwa kapolo**

Werengani Genesis 14.8-12

Kunali nkhondo. Loti ndi banja lake anatengedwa kapolo.

**7 February – Kumasulidwa**

Werengani Genesis 14.13-16

Abramu anamva kuti Loti ndi banja lake anatengedwa kapolo. Iye anatenga naye anthu ena. Anamasula banja la Loti ndi akatundu ao. Mulungu anasamalira Loti.

**8 February – Angelo awiri**

Werengani Genesis 19.1-3

Usiku wina angelo awiri anadza kwa Loti. Anafuna kukhala naye. Loti anawasamalira. Kodi mumasamalira alendo?

**9 February – Amuna a ku Sodomu**

Werengani Genesis 19.4-11

Usiku amuna a ku Sodomu anadza kwa Loti. Anafuna alendo awiri kuturuka m'nyumba. Anafuna kucimwa. Loti anakana. Anthu a ku Sodomu anakalipa kwambiri. Angelo anasamalira Loti.

**10 February – Kuthawa**

Werengani Genesis 19.12-23

Mulungu anafuna kulanga Sodomu koma kupulumutsa banja la Loti. Anayenera kuthawa. Kunali kobvuta kwa Loti. Angelo anamthandiza. Loti anayenera kufulumira kukapeza citetezo. Tifunika kupeza citetezo mwa Yesu mofulumira.

**11 February – Kuonongedwa**

Werengani Genesis 19.24-26

Mulungu anaononga Sodomu ndi Gomora. Mkazi wa Loti sanamvere. Analangidwa. Tiri pa ciopsezo cifukwa ca macimo athu. Tikalapa ku macimo athu ndi kukhulupirira mwa Yesu ndife otetezeka.

# Mulungu ndiye wolungama ndi wolunjika

Mulungu wokhulupirika ndi wopanda cisalungamo; Iye ndiye wolungama ndi wolunjika – Deuteronomo 32.4b

**12 February – Mulungu yekha ndiye wolunjika**

Werengani Aroma 3.10-18

M'nthano ya Loti Mulungu anaonetsa kuti Iye ndiye wolungama ndi wolunjika. Mulungu alanga anthu oipa ndipo apereka mphoto kwa abwino pa maso pake. Zimene Mulungu acita ndi zolunjika nthawi zonse. Mulungu yekha ndiye wolunjikadi.

Baibulo likamba kuti kulibe munthu aliyense amene ali wabwino pa maso pa Mulungu. Ife tonse tilephera kucita zimene Mulungu afuna. Tilephera pakuti mitima yathu ndi yocimwa. Ndife osalungama. Mulungu wolungama akuda cosalungama.

Tikalapa ku macimo ndipo tikakhulupirira Yesu monga Mpulumutsi wathu, Yesu atiyeretsa ku macimo athu ndi cosalungama cathu. Mwa Yesu tikhoza kukhala olungama pa maso pa Mulungu.

**Funso: Kodi ndinu wolungama pa maso pa Mulungu?**



**13 February – Cotsatira**

Werengani Aroma 1.18

Baibulo likamba kuti Mulungu akwiya kaamba ka cosalungama. Tifunika Yesu kucotsa macimo athu ndi mkwiyo wa Mulungu kaamba ka uchimo. Ngati macimo anu sadzakhululukidwa ndi Yesu pa nthawi ya imfa yanu, Mulungu sadzakulolani Kumwamba.

**14 February – Lapani**

Werengani Ezekieli 33.18 and 19

Mukalapa zoipa Mulungu adzakukhululukirani. Kulapa kutanthauza kumva cisoni pa zimene mwacita motsutsana ndi cifuniro ca Mulungu. Kutanthauzanso kuziulula kwa Mulungu ndi kuleka kucita zoipa.

**15 February – Wolungama mwa Yesu**

Werengani 2 Akorinto 5.20 and 21

Mwa imfa yake ya pa mtanda Yesu anasenza macimo (ndiwo cosalungama) a anthu ake. Iwo amene adalira pa Iye kuti apulumuke ku macimo ao ndiwo olungama pa maso pa Mulungu. Ndiwo olungama cifukwa ca zimene Yesu anawacitira.

**16 February – Cilungamo m'masiku onse**

Werengani Salimo 11.4-7

Mulungu afuna kuti anthu onse azicita zimene ziri zolungama. Mulungu atiphunzitsa m'Baibulo zimene ziri zabwino ndi zoipa. Yesu ndi citsanzo cathu cacikulu.

**17 February – Kulakalaka cilungamo**

Werengani Mateyu 5.1 and 2 and Matthew 5.6

Kodi mulakalaka cilungamo m'umoyo wanu wa masiku onse? Kodi mulakalaka kukhala wolungama pa maso pa Mulungu?

**18 February – Mulungu asamalira**

Werengani 1 Petro 3.8-12

Ngati mukhala wolungama pa maso pa Mulungu, Iye akusamalirani. Ngati simukhala wolungama pa maso pa Mulungu, Iye sakhala ndi inu. Adziwa zimene zicitika pa dziko lapansi. Tsiku lina adzaweruza anthu onse.

# Isake anamvera Mulungu

Ndikupatsani inu lamulo latsopano, kuti mukondana wina ndi mnzace; monga ndakonda inu, kuti inunso mukondane wina ndi mnzace – Yohane 13.34

**19 February – Mkazi wa Isake**


Werengani Genesis 24.1-9

Sara, mkazi wa Abrahamu, adafa kale. Abrahamu anakalamba. Isake anali mphatso yapadera yomwe Mulungu anapatsa Abrahamu ndi mkazi wake. Patapita zaka zambiri Ambuye Yesu adzabadwa ku mbeu ya Abrahamu ndi Isake.

Abrahamu anafuna kuti mwana wake Isake akwatire. Sanafune Isake kukwatira mkazi wa ana akazi Akanani. Akanani sanatumikire Mulungu. Isake anayenera kukwatira mkazi wokonda Mulungu. Tiyenera kukhala ocenjera pa mkazi (mwamuna) yemwe tikwatira (tikwatiwa). Kukwatira (kapena kukwatiwa) munthu amene sali Mkristu kutibvutitsa.

Abrahamu anatuma mnyamata wamkulu wa pa nyumba yace kuti apeze mkazi wa Isake. Anakhulupirira kuti Mulungu adzamthandiza kupeza mkazi wabwino.

**Funso: Ndi ciani cimene ciri cofunikira pa ukwati kulingana ndi inu?**



**20 February – Pemphero**

Werengani Genesis 24.10-14

Poyambayamba mnyamata anapemphera. Pemphero ndi lofunikira ngati mufunafuna munthu wokwatira (kapena wokwatiwa). Mutayamba ukwati mupitirize kupempherera.

**21 February – Pemphero linayankhidwa**

Werengani Genesis 24.15-27

Mulungu anayankha pemphero mosacedwa. Mulungu amamva mapemphero athu. Awayankha m'njira yabwino yoposa kulingana ndi Iye. Mnyamata analemekeza Mulungu pa yankho lake.

**22 February – Ku nyumba ya Lababi**

Werengani Genesis 24.28-33 and 24.50-53

Labani, mlongo wa Rebeka, anaitana mnyamata ku nyumba yake. Kumeneko mnyamata anafotokoza njira imene Mulungu adayankha pemphero lake.

**23 February – Rebeka**

Werengani Genesis 24.54-61

Rebeka anamvetsa kuti Mulungu afuna iye kukhala mkazi wa Isake. Anafuna kumvera Mulungu ndi kucita cifuniro cake.

**24 February – Kukwatirana**

Werengani Genesis 24.62-67

Isake ndi Rebeka anakwatirana. Analandirana monga mphatso yocokera kwa Mulungu. Kodi muona mwamuna/mkazi wanu monga ndiye mphatso yocokera kwa Mulungu?


**25 February – Citsanzo**

Werengani Aefeso 5.22-28

Ukwati uzikhala citsanzo ca ubwenzi pakati pa Mulungu ndi anthu ake. Mkazi azipereka kwa mwamuna wake monga ana a Mulungu adzipereka kwa Mulungu. Mwamuna azicitira zabwino mkazi wake monga Mulungu amacitira anthu ake.

# Yakobo ananyenga tate wake

Zakudya za cinyengo zikondweretsa munthu; Koma pambuyo pace m'kamwa mwace mudzadzala tinsangalabwi – Miyambi 20.17



**26 February – Yakobo ndi Esau**

Werengani Genesis 25.19-28

Isake ndi Rebeka anakwatirana. Analibe mwana. Ico ndi cacisoni kwambiri. Isake anapemphera Mulungu kulandira mwana. Tiloledwa kupempha Mulungu ciriconse comwe tifunika.

Mulungu anayankha pemphero la Isake. Rebeka anali ndi pakati; mapasa. Iwo, ana a amuna anabvutitsana asanabadwe. Rebeka anadabwa. Anafunsa Mulungu za ico. Mulungu ananena kuti iwo adzamenyana kwambiri. Ngakhale mbeu yao idzadana. Kudzakhala mitundu iwiri.

Wobadwa woyamba ndiye Esau. Wobadwa waciwiri ndiye Yakobo. Isake, tate wao anakonda Esau kwambiri. Rebeka, mai wao anakonda Yakobo kwambiri.

**Funso: Kodi mumacita ciani pamene mufuna ciriconse?**

**27 February – Dalitso lalikulu**

Werengani Genesis 25.29-34

Esau anapempha Yakobo cakudya. Yakobo anati kuti afuna kupatsa cabe ngati Esau amupatsa dalitso lalikulu. Dalitso lalikulu linali la ana obadwa oyamba. Esau sanalabadire dalitso la Mulungu.

**28 February – Isake anafuna kudalitsa Esau**

Werengani Genesis 27.1-5

Tate Isake anadziwa kuti adzafa. Anafuna kudalitsa mwana wa mwamuna wake Esau ndi dalitso lalikulu. Anamuuza kupita kuthengo kukapeza nyama ndiponso kumukonzekera cakudya. Atacita tero adzadalitsidwa ndi tate Isake.

**29 February – Ganizo la Rebeka**

Werengani Genesis 27.6-17

Rebeka anamva zimene Isake ananena. Anadziwa kuti Yakobo anayenera kudalitsidwa. Anapanga ciwembu ca kunyenga Isake. Ico cinali coipa. Rebeka anayenera kuyembekezera nthawi ya Mulungu.

**1 March – Yakobo anadalitsidwa ndi Isake**

Werengani Genesis 27.18-29

Yakobo anapita kwa tate wake Isake ndipo anacita monga ndiye Esau. Isake anadalitsa Yakobo. Kunena bodza ndiko chimo. Mulungu afuna kuti tizikhala oona. Kodi ndinu wosanama?

**2 March – Esau anafunanso dalitso**

Werengani Genesis 27.30-40

Esau anacokera kuthengo. Isake adadalitsa kale Yakobo. Esau anafunanso dalitso. Analira. Anali wacisoni kwambiri ndi wodzadza ndi maganizo wopweteka pa zimene zidacitika.

**3 March – Yakobo anayenera kuthawa**

Werengani Genesis 27.41-46

Esau anakwiya kwambiri. Yakobo anayenera kuthawa kukapeza citetezo. Chimo libweretsa mabvuto pa anthu nthawi zonse. Kodi ndi chimo lotani m’umoyo wanu limene likubvutitsani?

# Mulungu anasamalira Yakobo

Inu Yehova, simudzandikaniza nsoni zanu: Cifundo canu ndi coonadi canu zindisunge cisungire – Salimo 40.11

**4 March – Mulungu ndi wacifundo**

Werengani Genesis 28.10-22

Cifukwa ca chimo lake Yakobo anayenera kuthawa. Adanyenga tate wake. Mphwace anakalipa kwambiri naye. Yakobo anali yekha. Usiku wina Mulungu anadzibvumbulutsira Yakobo. Mulungu analonjeza kumusamalira, ngakhale adacimwa. Yakobo sanali yekha. Mulungu anali naye. Atauka Yakobo anadabwa. Sanayembekeza Mulungu kukhala naye. Anadabwa kuti Mulungu ndiye wacifundo kwambiri. Yakobo anayamika ndipo anakonda Mulungu. Anacha malo ao Beteli. Analonjeza kubweranso ngati Mulungu adzamusamalirabe.

**Funso: Kodi mumayankha bwanji cifundo ca Mulungu?**



## 5 March – Yakobo anakwatira Leya

Werengani Genesis 29.13-24

Yakobo anafika ku nyumba ya Labani. Anabvomerezana ndi Labani kukwatira mwana wa mkazi wake atagwira nchito zaka zisanu ndi ziwiri. Labani anamupatsa mwana wa mkazi wake wina, Leya. Yakobo ananyengedwa ndi Labani.

## 6 March – Yakobo anakwatira Rakele

Werengani Genesis 29.25-30

Yakobo anagwiranso nchito zaka zisanu ndi ziwiri kuti akwatire Rakele. Anakonda Rakele kuposa Leya.

## 7 March – Yakobo anabweranso

Werengani Genesis 31.3, 17 ndi 18

Mulungu anauza Yakobo kubweranso ku dziko la tate wake Isake. Dzina la dzikolo ndi Kanani. Yakobo anapita ndi akazi ake, ana ake ndi akatundu. Mulungu analonjeza kukhala naye. Kodi Mulungu akhalanso ndi inu?

## 8 March – Mulungu analimbikitsa Yakobo

Werengani Genesis 32.3-8 ndi 32.24-32

Yakobo anaopa mphwace Esau. Anapempha Mulungu thandizo. Anatumiza mphatso kwa Esau. Usiku Mulungu anadza kwa Yakobo kumulimbikitsa. Mulungu anamupatsa dzina latsopano. Ana a Yakobo ndiwo Aisrayeli.

## 9 March – Yakobo anakomana ndi Esau

Werengani Genesis 33.1-4

Mulungu anayankha pemphero la Yakobo. Esau sanakhalebe wokalipa. Pamene tiri ndi bvuto ndi munthu wina, tizilakalaka kuyanjana nthawi zonse.

## 10 March – Kubweranso kwa Beteli

Werengani Genesis 35.1-5

Mulungu anauza Yakobo kubwereranso kwa Beteli. Anatenga banja lake. Iwo onse anataya mafano onse. Anafuna kumvera Mulungu yekha. Kodi muli ndi mafano?

# Yosefe m'mabvuto

Ndi kutaya pa Iye nkhawa yanu yonse, pakuti Iye asamalira inu – 1 Petro 5.7



**11 March – Yosefe anadedwa ndi abale ake**

<u>Werengani Genesis 37.1-11</u>

Cingacitike kuti makolo akonda mwana wao umodzi kuposa ana ao ena. Ici cibvutitsa: ana ayamba kudana. Ico cinacitika m'umoyo wa Yosefe.

Yakobo, tate wa Yosefe, anakwatira Rakele ndi Leya. Yakobo anali ndi ana a amuna khumi imodzi ndi awiri ndi mwana wa mkazi umodzi. Rakele anali mai wake wa Yosefe ndi Benjamini. Yakobo anawakonda kuposa ana ake ena a Leya. Cifukwa ca ici Yosefe anadedwa ndi abale ake.

Yosefe anauza abale ake loto lake. Adawaona akumugwadira monga ndiye mfumu. Abale ake anamuda kwambiri. Umoyo sunali pafupi ndi Yosefe. Koma Mulungu anamusamalira.

**Funso: Kodi mumacita ciani pamene anthu ena akubvutitsani?**

**12 March – Yosefe m'dzenje**

Werengani Genesis 37.18-28

Abale a Yosefe anafuna kumupha. Rubeni, m'bale wamkulu, sanafune tero. Cifukwa ca ici anamuponya Yosefe m'dzenje. Patapita nthawi, Yosefe anagulitsidwa natengedwa ku Aigupto. Tizithandiza anthu nthawi zonse, monga Rubeni anacita.

**13 March – Abale ananena bodza**

Werengani Genesis 37.29-36

Abale a Yosefe anauza tate wao kuti Yosefe anaphedwa ndi nyama. Iyo inali bodza. Tinganyenge anthu ena, koma Mulungu adziwa coonadi nthawi zonse. Kodi mwanyenga anthu ena?

**14 March – Yosefe m'Aigupto**

Werengani Genesis 39.1-20

Yosefe anakana kucimwa. Anaponyedwa m'ndende cifukwa ca chimo limene sanalicite. Ngakhale tikamvera Mulungu tingabvutike. Tiyenera kuuza Mulungu za zonse zimene zitibvutitsa.

**15 March – Yosefe m'ndende**

Werengani Genesis 39.21-23

Yosefe sanataye mtima wake m'ndende pakuti Mulungu anamusamalira. Yosefe analoledwa kuthandiza woyang'anira kaidi. Woyang'anira kaidi anaona kuti Yosefe anali munthu wabwino woposa andende ena.

**16 March – Yosefe anapempha thandizo**

Werengani Genesis 40.1-15

Ndi thandizo la Mulungu Yosefe anamasulira loto la wopereka cikho. Yosefe anamufunsa kuti akamunenere zabwino pamene woperekayo cikho adzamasulidwa.

**17 March – Yosefe anaiwalidwa**

Werengani Genesis 40.16-23

Yosefe anauzanso citanthauzo ca loto la wophika mkate. Zonse zinacitika monga Yosefe adawauza. Wopereka cikho sanacite zimene adalonjeza. Anaiwala Yosefe. Mulungu sanaiwale Yosefe.

# Yosefe ndi abale ake anayanjananso

Koma mukhalirane okoma wina ndi mnzace, a mtima wacifundo, akukhululukirana nokha, monganso Mulungu mwa Kristu anakhululukira inu – Aefeso 4.32

**18 March – Maloto a Farao**


<u>Werengani Genesis 41.14-24</u>

M'loto wace mfumu wa Aigupto anaona ng'ombe zisanu ndi ziwiri zimene zinaturuka m'madzi. Zinaoneka zathanzi: zazikulu ndi zonenepa. Kenaka anaona zisanu ndi ziwiri zina zocokera m'madzi. Izo zinaoneka zoonda. Ng'ombe zoonda zinadya ng'ombe zathanzi koma zinakhalabe zoonda.

Mfumu analotanso. Anaona ngala zisanu ndi ziwiri zabwino zimene zinadya ngala zisanu ndi ziwiri zoonda. Mfumu anadabwa cifukwa ca maloto. Kunalibe munthu amene angamuuze citanthauzo.

Pamene wopereka cikho anauza mfumu za Yosefe, Yosefe anaitanidwa kuti afotokoze citanthauzo ca maloto a mfumu. Yosefe sanabwezere wopereka cikho pa kumuiwala. Yosefe anali munthu wokoma mtima ndi wa mtima wacifundo.

**Funso: Kodi ndinu wokoma ndi wa mtima wacifundo?**



**19 March – Citanthauzo ca maloto**

Werengani Genesis 41.25-32

Ndi thandizo la Mulungu, Yosefe anamasulira loto la mfumu Farao. Patapita zaka zisanu ndi ziwiri zabwino ndi zakudya zambiri kudzakhala zaka zoipa. Kudzakhala njala.

**20 March – Kumasulidwa m'ndende**

Werengani Genesis 41.39-46

Mfumu Farao anafuna Yosefe kumuthandiza. Yosefe anayenera kumanga malo osungiramo cakudya kuti kudzakhala cakudya pa nthawi ya njala. Mulungu anafuna Yosefe kuthandiza mfumu. Yosefe anamvera Mulungu amene ali Mfumu ya mafumu.

**21 March – Abale a Yosefe**

Werengani Genesis 42.6-20

Abale a Yosefe anacokera m'dziko la Kanani kugula cakudya. Sanazindikire Yosefe. Yosefe anawayesa podziwa ngati adasintha makhalidwe ao oipa.

**22 March – Abale anamva cisoni pa chimo lao**

Werengani Genesis 42.21-25

Abale a Yosefe anayamba kuzindikira kuti adacitira zoipa Yosefe. Titacita coipa tiyenera kuciulula. Kodi kuli chimo lomwe muyenera kuulula lero?

**23 March – Yosefe anadzibvumbulutsa**

Werengani Genesis 45.1-15

Zinthu zambiri zinacitika. Pa nthawi ina Yosefe anauza abale ake kuti ndiye Yosefe. Abale anaopa kuti angawalange. Yosefe sanacite tero. Anawakhululukira. Tiyeneranso kukhululukirana.

**24 March – Abale a Yosefe anaulula bodza lao**

Werengani Genesis 45.25-28

Abale anafotokoza atate ake zimene zidacitika ku Aigupto. Anafotokozanso kuti adamunyenga. Ifenso tiyenera kuulula ndi kulapa ku macimo athu.

# Cikondi ca Mulungu

Tikonda ife, cifukwa anayamba Iye kutikonda – 1 Yohane 4.19



**25 March – Mulungu ndiye cikondi**

Werengani 1 Yohane 4.7-10

Sabata latha tinawerenga nthano ya Yosefe. Yosefe anakonda abale ake. Baibulo likamba kuti ciyambi ca cikondi ceniceni ndico Mulungu. Mulungu ndiye cikondi.

M'umoyo wathu wa masiku onse tikonda anthu ena kaamba ka zifukwa zosiyanasiyana. Nthawi zambiri tikonda anthu amene atipatsa cinthu, monga cakudya, tsogolo, malo okhalako, zobvala kapena zinthu zina. Nthawi zambiri kukonda kumakhalapo ngati pali kupatsidwa.

Cikondi ca Mulungu ndi cosiyana ndi cikondi ca anthu. Iye satikonda cifukwa ca cimene timupatsa. Apatsa mwa cikondi. Cikondi ca Mulungu ndi caulere. Cikondi cake ndi cifundo ceniceni. Mwa cikondi afuna kupulumutsa anthu opandukira akukhala otayika kopanda Iye (Yohane 3.16).

**Funso: Kodi cikondi ca Mulungu citanthauza ciani kwa inu?**

**26 March – Lamulo la Mulungu**

Werengani Mateyu 22.37-40

Mulungu afuna kuti timukonde. Iye ndiye Mlengi wathu. Ayenera cikondi cathu ndi matamando athu. Afunanso kuti tizikonda munthu wina aliyense.

**27 March – Mulungu asankha kukonda**

Werengani Deuteronomo 7.6-8

Mulungu sanakonde Aisrayeli pakuti ndiwo anthu opambana. Mulungu anawakonda cifukwa anafuna kuwakonda.

**28 March – Cikondi copulumutsa**

Werengani Aroma 5.6-8

Yesu Kristu sanafe kupulumutsa anthu opambana. Anafa kupulumutsa anthu osalungama, opanda mphamvu ndi ocimwa. Anafa kuti iwo akhale abwenzi a Mulungu mwa Iye. Cikondi cake ndi codabwitsa!

**29 March – Kukonda adani**

Werengani Mateyu 5.43-48

Mulungu afuna kuti tizikonda anthu onse. Ngakhale adani athu. Mulungu akonda anthu ocimwa (adani ake) ndipo tiyenera kucita cimodzi-modzi. Yesu ndiye citsanzo cathu.

**30 March – Kukonda Mulungu**

Werengani 1 Yohane 4.19-21

Cikondi cathu ca Mulungu ndico cotsatira ca cikondi cake ca ife. Cikondi cathu ca Mulungu ndico mphatso yocokera kwa Mulungu. Mulungu atipatsa zonse zimene tifunika kuti timutumikire. Kodi mumakonda Mulungu?

**31 March – Cikondi cocita**

Werengani 1 Yohane 3.16-18

Cikondi si kumva kapena liu cabe. Kukonda kutanthauza kucita zabwino ndiponso kucitira anthu onse zabwino zoposa. Osaganizira zimene mungalandire, koma zimene mungapatse. Kodi mungathandize bwanji anthu a pafupi ndi inu?

# Mose, mtumiki wa Mulungu

## Kuti mudziwe kuti Ine ndine Yehova – Eksodo 10.2b











**1 April – Kubadwa kwa Mose**

<u>Werengani Eksodo 2.1-10</u>

Yosefe adafa m'Aigupto. Iye ndi abale ake anali ndi ana ambiri. Anachedwa Aisrayeli. Kunali mfumu watsopano m'Aigupto. Sanakonde Aisrayeli. Anawapangitsa kukhala akapolo. Ana a amuna akhanda a Aisrayeli onse anaphedwa. Atabadwa Mose mai wake anamubisa. Mwana wamkazi wa Farao anamupeza. Mose analeredwa monga Maigupto m'nyumba ya mfumu. Mulungu anafuna kuti Mose apulumuke cifukwa anafuna kumuika pa udindo wapadera.

**Funso: Kodi Mulungu akuikani pa udindo wotani m'umoyo wanu?**

**2 April – Mose anayenera kuthawa**

Werengani Eksodo 2.11-15

Mose anakonda Aisrayeli. Anadziwa kuti kukhala pamodzi ndi anthu obvutika a Mulungu ndiko kwabwino kuposa kukhala wolemera wopanda Mulungu (Ahebri 11.24-26). Kodi ndi ciani ca izi ziwiri cimene mukonda koposa?

**3 April – Mulungu anaitana Mose**

Werengani Eksodo 3.1-14

Mulungu anamva mapemphero a Aisrayeli. Anauza Mose kuwaturutsa m'Aigupto nawalowetsa m'Kanani. Mulungu analonjeza kupita nao. Kodi Mulungu alinso ndi inu?

**4 April – Mose ndi Aroni pa maso pa mfumu**

Werengani Eksodo Exodus 5.1 ndi 2 ndiponso 7.1-6

Mose ndi m'bale wake Aroni anapita kwa mfumu wa Aigupto kumupempha cilolezo kuti awatulutse. Mfumu anakana. Mukacita cifuniro ca Mulungu mukomana ndi anthu otsutsa ndi inu nthawi zambiri.

**5 April – Zozizwitsa**

Werengani Eksodo 7.14-25

Mulungu analanga Aaigupto cifukwa sanalole Aisrayeli kucokako. Madzi anasanduka mwazi. Mfumu anakanabe kumvera Mulungu, ndiye Mulungu anacita zozizwitsa zina (Eksodo 8, 9 ndi 10). Kodi mumamvera Mulungu?

**6 April – Mwazi pa mphuthu**

Werengani Eksodo 12.1-13

Aisrayeli amene anapaka mwazi wa mwana wa nkhosa pa mphuthu za nyumba zao anatetezeka m'nyumba zao. Mwana wa nkhosa anafa kuti wobadwa woyamba atetezeke. Ici citikumbutsa za Yesu. Anafa kupulumutsa ana ake ku mkwiyo wa Mulungu.

**7 April – Kumasulidwa m'Aigupto**

Werengani Eksodo 12.29-36

Obadwa oyamba ambiri a Aisrayeli anaphedwa cifukwa nyumba zao zinali zopanda mwazi pa mphuthu. Aisrayeli analoledwa kuturuka ndiponso kutenga nao ciriconse cimene afuna.

# Ulendo wa m'cipululu

Muziyenda kutsata Yehova Mulungu wanu, ndi kumuopa

Deuteronomo 13.4a


**8 April – Mulungu anasamalira anthu ake**

<u>Werengani Eksodo 13.21-22 ndi 15.22-25</u>

Aisrayeli anaturuka m'Aigupto nayamba ulendo wao ku Kanani, dziko la malonjezano. Mulungu anagwiritsa nchito mtambo kuwaonetsa njira. Usana mtambo unawacinga. Usiku unaunikira kuwateteza. Mulungu anakhala nao tsiku lonse. Ngati Mulungu akhala nanu ndinu otetezeka nthawi zonse.

Ngakhale Mulungu ali nanu mungabvutike. Aisrayeli anakomananso ndi bvuto. Madzi anali owawa. M'malo mwa kudandaula anayenera kupemphera. Kudandaula ndi chimo. Ngakhale Aisrayeli anacimwa, Mulungu awathandiza. Anasandutsa madzi kuti akhale okoma. Mulungu anawasamalira. Atisamaliranso. Amasamalira makamaka ana ake.

**Funso: Kodi muona bwanji cisamaliro ca Mulungu m'umoyo wanu?**



**9 April – Kudandaula**

Werengani Eksodo 16.1-12

Mulungu adasamalira Aisrayeli. Koma iwo anadandaulanso. Anafuna kukhala ndi cakudya cabwino. Mulungu ndi wacisomo. Analonjeza kuwapatsa cimene anafuna.

**10 April – Mkate wa Kumwamba**

Werengani Eksodo 16.13-21

Mulungu anapatsa aliyense cakudya. Kunali cakudya cokwanira kukhuthitsa. Mulungu anawauza kuti asacisunge. Adzapatsa masiku onse. Cakudya ndi mphatso yomwe Mulungu atipatsa. Kodi mwalandira cakudya cotani cocokera kwa Mulungu?

**11 April – Tsiku lacisanu ndi ciwiri**

Werengani Eksodo 16.22-31

Mulungu anafuna kuti anthu apumula pa tsiku lacisanu ndi ciwiri. Pa tsiku lacisanu ndi cimodzi anawapatsa cakudya cokwanira masiku awiri. Mulungu akondwera pamene timumvera.

**12 April – Mulungu ndi wamphamvu koposa**

Werengani Eksodo 17.8-13

Mulungu anaonetsa kuti ndiye wamphamvu kuposa adani. Mulungu ndi wamphamvu kuposa anthu onse. Ngakhale m'umoyo wathu. Tiyenera kumupempha mphamvu yake kuti timenyere uchimo ndi Satana.

**13 April – Malamulo khumi**

Werengani Eksodo 20

Aisrayeli anamva mantha pamene Mulungu anadzibvumbulutsa. Mulungu ndiye wamkulu ndi woyera ndipo anthu ndiwo ocimwa. Anawapatsa malamulo ake kuti Aisrayeli amumvere. Cifukwa ca malamulo khumi tidziwa kuti ndife ocimwadi.

**14 April – Kusamvera Mulungu**

Werengani Eksodo 32.1-14 ndi 32.30-35

Aisrayeli anapanga fano la mwana wa ng'ombe wa golide. Anati kuti ndilo milungu yao. Anaiwala lonjezo lao lotumikira Mulungu. Mulungu anakalipa. Salola chimo lirilonse. Tifunika mphamvu ya Mulungu kuti timutumikire.

# M’cipululu

Amene anatsogolera anthu ake m’cipululu: Pakuti cifundo cace ncosatha – Salimo 136.16



**15 April - Nsanje**

Werengani Numeri 12.1-9

Miriamu ndi Aroni anacita kaduka. Sanakonde Mose kukhala mtsogoleri wamkulu wa Aisrayeli. Anaganiza kuti iwonso ndiwo ofunikira. Kukhala wodzikweza ndi ansanje ndiko chimo. Mose sanakwiye. Anali woleza mtima. Koma Mulungu anakwiya. Anafotokoza kuti adasankha Mose kukhala mtsogoleri.

**Funso: Kodi ndinu munthu wansanje?**

**16 April – Cilango**

Werengani Numeri 12.10-16

Miriamu anadwala cifukwa ca chimo lake. Aroni anaopa. Mose anapempherera Miriamu. Anafunsa Mulungu kumuciritsa. Mose anali wokoma mtima. Kodi mumayankha bwanji pamene anthu akhala ansanje?

**17 April – Azondi**

Werengani Numeri 13.17-25

Mose anatuma azondi ku Kanani. Anafuna kuti aone kuti dziko lioneka lotani. Dziko linali labwino kwambiri. Kunali zipatso zambiri. Mulungu anawalonjeza dziko labwino kwambiri.

**18 April – Azondi anasimba**

Werengani Numeri 13.26-33

Azondi ena ananena kuti sadzakwaniritsa kugonjetsa anthu a ku Kanani. Ena anati kuti Mulungu adzawathandiza pakuti Mulungu anawalonjeza dziko. Kodi mumakhulupirira zimene Mulungu akamba kapena zimene anthu akamba?

**19 April – Cilango ca Mulungu**

Werengani Numeri 14.1-10

Aisrayeli analibe ciyembekezo. Anafuna kubwereranso ku Aigupto. Mulungu analanga Aisrayeli cifukwa sanadalire mphamvu yake. Anayenera kuyendayenda m'cipululu zaka 40 (Numeri 14.33).

**20 April – Njoka**

Werengani Numeri 21.4-9

Aisrayeli anadandaula cifukwa ca cakudya cimene Mulungu anawapatsa. Mulungu anawalanga ndi njoka. Aisrayeli anapemphera. Mulungu anaciritsa iwo openya njoka yamkuwa. Munthu aliyense wopenya Yesu aciritsidwa ku uchimo.

**21 April – M'Kanani**

Werengani Yoswa 6.2-16 ndi 6.20

Aisrayeli anakhala m'cipululu zaka zambiri. Kunacitika zambiri. Anthu ambiri anafa. Patapita zaka 40 Mulungu anawapatsa dziko la malonjezano. Mzinda woyamba womwe anagonjetsa unali Yeriko. Mulungu acita zimene alonjeza.

# Mulungu ndiye woyenerera

Woyera, woyera, woyera, Ambuye Mulungu Wamphamvuyonse, amene anali, amene ali ndi amene alinkudza – Cibvumbulutso 4.8b

**22 April – Mneneri Yesaya anaona Mulungu**

Werengani Yesaya 6.1-5

Masabata atha tinawerenga kuti Aisrayeli m'cipululu analangidwa cifukwa ca macimo ao. Anthu ali ndi macimo, koma Mulungu alibe chimo lirilonse. Mulungu ndiye woyera. Ici citanthauza kuti Mulungu ndiye wolungama, wopanda koipa, wolemekezeka, wamkulu ndi wamphamvu yonse. Mulungu ndi wosiyana ndi anthu. Pamene mneneri Yesaya anaona Mulungu anamvetsa kuti Mulungu ndiye woyera. Mulungu ndiye woyera kwambiri kuti ngakhale angelo anaphimba nkhope zao. Anaopa Mulungu. Mneneri Yesaya anadziwa kuti iye yemwe si ndiye wabwino. Anaopa kuti angafe pakuti Mulungu ndiye woyera ndipo iye si ndiye woyera. Mneneri Yesaya anadzicepetsa.

**Funso: Kodi kutanthauza ciani kwa inu kuti Mulungu ndiye woyera?**



**23 April – Lemekezani Mulungu**

Werengani Salimo 99

Mulungu ndiye Mfumu wa dziko lonse lapansi. Anthu onse ayenera kudzicepetsa ndi kulemekeza Mulungu. Ici ndi colinga ca miyoyo yathu. Tiyenera kutumikira ndi kutamandira Mulungu m'zonse zomwe ticita.

**24 April – Mulungu aona zonse**

Werengani Salimo 11.4-7

Mulungu ali Kumwamba. Aona ndipo adziwa zonse zimene anthu acita. Adziwa ngati mumumvera. Adziwa pamene mucimwa.

**25 April – Kulemekeza Mulungu pa ciyero cake**

Werengani 1 Samueli 2.1 and 2

Pamene Hana anapemphera anaulula kuti Mulungu ndiye woyera. Kulibe wina aliyense monga Mulungu. Kodi mumalemekeza Mulungu pa ciyero cake?

**26 April – Mau a Mulungu ndi oyera**

Werengani Salimo 19.7-9

Mulungu yemwe ndiye woyera. Mau a Mulungu, Baibulo, ndiwonso oyera. Ndi Buku lapamwamba kwambiri.

**27 April – Kukhala woyera mwa Yesu**

Werengani 1 Akorinto 6.9-11

Anthu okhululukidwa ku macimo ao ndi mwazi wa Yesu ndiwo oyera pa maso pa Mulungu. Sakwaniritsa kukhala umoyo woyera pa okha. Afunika mphamvu ya Mulungu kuti agonjetse uchimo ndiponso kuti ayetsetse ciyero.

**28 April – Khalani umoyo woyera**

Werengani 1 Petro 1.14-16

Mulungu afuna Akristu kukhala monga Iye. Iwo ayenera kukhala umoyo woyera. Azikhala osiyana ndi anthu amene sadziwa Mulungu. Akristu azicita zimene Mulungu afuna nthawi zonse.

# Umoyo wa Samsoni

Koma mumuope Yehova, ndi kumtumikira koona, ndi mtima wanu wonse – 1 Samueli 12.24a

**29 April – Mwana analonjezedwa**

Werengani Oweruza 13.1-14

Aisrayeli anaiwala za Mulungu. Anapembeza mafano. Mulungu anatuma Afilisti kuwamenyera. Aisrayeli anabvutika. Manowa ndi mkazi wake anali Aisrayeli. Analibe mwana. Tsiku lina Mngelo anauza mkazi wa Manowa kuti adzakhala ndi mwana. Mngelowo anali Mulungu yemwe. Mwana wao Samsoni adzatumikira Mulungu napulumutsa Aisrayeli m'dzanja la Afilisti. Cifukwa ca ici sanaloledwe kumwa coledzeretsa. Ndipo asametedwe tsitsi lake. Izi zinali zozindikira za kutumikira Mulungu. Pamene Manowa anamva izi anafuna kumvanso uthenga wa Mngelo. Anapempha Mulungu. Mulungu anayankha pemphero lake. Mngelo anadza kumuuza za mwana amene adzabadwa.

**Funso: Kodi kutumikira Mulungu kutanthauza ciani kwa inu?**



**30 April – Nsembe ya Mulungu**

Werengani Oweruza 13.15-25

Manowa anapereka nsembe ya mbuzi. Mngelo anacokako. Manowa ndi mkazi wake anazindikira kuti ndiye Mngelo wa Mulungu. Anaopa. Kodi mungamve bwanji kukapezeka pamodzi ndi Mulungu?

**1 May – Mkazi wa ana akazi a Afilisti**

Werengani Oweruza 14.1-9

Samsoni anafuna kukwatira Mfilisti. Iye ndi makolo ake anapita kumuona. Samsoni anapha mkango. Anali wamphamvu. Atapita masiku Samsoni anapeza mtembo wa mkango ndi njuci m'mtembowo. Sanauze munthu aliyense za ici.

**2 May – Ukwati**

Werengani Oweruza 14.10-20

Samsoni anawaphera chilape. Oitanidwa ku ukwati anadziwa yankho cifukwa mkazi wa Samsoni adawauza. Samsoni anakalipa. Anapha Afilisti 30. Anapatsa zobvala zao kwa alendo a ukwati.

**3 May – M'Gaza**

Werengani Oweruza 16.1-3

Usiku Samsoni anakhala m'nyumba ya mkazi wadama. Ico cinali chimo. Afilisti anabwera kugwira Samsoni. Iye anathawa. Samsoni anali wamphamvu kwambiri. Mulungu anamupatsa mphamvu yomenyera Afilisti.

**4 May – Delila**

Werengani Oweruza 16.4-21

Delila anafuna kuthandiza Afilisti kuti agwire Samsoni. Anamumeta. Samsoni analibe mphamvu. Anagwiridwa ndi Afilisti. Afilisti anakolowola maso ake. Mulungu salola chimo lirilonse.

**5 May – Imfa ya Samsoni**

Werengani Oweruza 16.22-31

Mulungu analinso ndi Samsoni. Samsoni anapempha Mulungu mphamvu kuti aphe Afilisti. Anthu ambiri anafa. Samsoni anafanso. Kwa Samsoni ulemerero wa Mulungu unali wofunikira wuposa moyo wake. Ndi ciani cimene ciri cofunikira kulingana ndi inu?

# Sankho la Rute

Ndipo onse amene adasiya nyumba, kapena abale, kapena alongo, kapena atate, kapena amai, kapena ana, kapena minda, cifukwa ca dzina langa, adza-landira zobwezeredwa zambirimbiri nadzalowa moyo wosatha – Mateyu 19.29

**6 May – M'Moabu**


Werengani Rute 1.1-5

Aisrayeli anapitiriza kusamvera Mulungu. Mulungu anawalanga ndi njala. Anthu onse anali ndi njala.

Elimeleki ndi mkazi wake Naomi anapanga maganizo kuti apite ku dziko lina. Anapita ku Moabi. Ku Moabu kunali cakudya. Anapita ndi ana ao Maloni ndi Kilioni.

Elimeleki anafa m'Moabu. Maloni ndi Kilioni anakwatira. Akazi ao anali Olipa ndi Rute. Anakhala m'dziko la Moabu zaka 10. Mahloni ndi Kilioni anafanso.

**Funso: Ndi cifukwa ciani tiyenera kupempha thandizo kwa Mulungu pamene tipanga maganizo?**



## 7 May – Sankho la Rute

Werengani Rute 1.6-14

Naomi anafuna kubweranso ku Israyeli. Njala inali itatha. Anauza apongozi ake kukhala m'Moabu. Olipa anasankha kukhala. Rute anafuna kupita ndi Naomi.

## 8 May – Sankho la Rute

Werengani Rute 1.15-18

Rute anafuna kukhala pamodzi ndi Aisrayeli. Anafuna kutumikira Mulungu. Sanafunebe kutumikira mafano a ku Moabu. Kodi mufuna kutumikira yani?

## 9 May – Naomi ndi Rute anafika

Werengani Rute 1.19-22

Naomi ndi Rute anafika ku Israyeli. Anthu anaona kuti Naomi adabvutika. Naomi anasintha dzina lake cifukwa ca mabvuto amene adakomana nao. Anakhala ku Betelehemu.

## 10 May – M'munda

Werengani Rute 2.1-3

Rute anasamalira Naomi. Anapita ku munda kukapeza cakudya. Anagwira nchito m'munda wa Boazi. Kodi mumasamalira bwanji banja lanu?

## 11 May – Boazi ndi Rute

Werengani Rute 2.4-13

Boazi anamva kuti Rute anasamalira Naomi. Anakondwera pa kumva ico. Analola Rute kukhala m'munda wake kuti apeze cakudya. Rute anadabwa kuti Boazi anali wokoma mtima kwa iye.

## 12 May – Mulungu anasamalira

Werengani Rute 2.14-23

Naomi anakondwera kwambiri pamene Rute anamuuza za Boazi. Mulungu anawasamalira. Patapita nthawi Boazi anakwatira Rute (Rute 3 ndi 4).

# Yobu m'mabvuto


Koma cipulumutso ca olungama cidzera kwa Yehova, Iye ndiye mphamvu yao m'nyengo ya nsautso – Salimo 37.39

**13 May – Yobu wolemera**

<u>Werengani Yobu1.1-5</u>

Baibulo likamba kuti Yobu ankamvera Mulungu. Sanalakwe. Analemekeza Mulungu. Anakonda Mulungu. Yobu analemera kwambiri. Anali ndi nyama zambiri. Yobu anakwatira nakhala ndi ana 10. Ana ake anacita madyerero pamodzi. Yobu anaopa kuti angacimwe. Anawapempherera.

**Funso: Kodi mumapempherera yani?**



**14 May – Ciwembu ca Satana**

Werengani Yobu 1.6-12

Satana amada Mulungu ndi anthu a Mulungu. Anati kuti Yobu sangatumikire Mulungu akakhala osauka. Mulungu analola Satana kucotsa akatundu a Yobu. Satana akwaniritsa cabe cimene Mulungu amulola kucita. Ngakhale m'miyoyo yathu.

**15 May – Yobu anataya zonse**

Werengani Yobu 1.13-19

Yobu anataya zonse zimene anali nazo. Nyama zake zonse zinafa ndipo ana ake onse anafa. Ndi cacisoni kwambiri!

**16 May – Yankho la Yobu**

Werengani Yobu 1.20-22

Yobu anamva cisoni cacikulu pa zimene zidacitika. Komabe analemekeza Mulungu. Kodi mumacita ciani mukabvutika?

**17 May – Ciwembu cina**

Werengani Yobu 2.1-10

Satana anaona kuti Yobu anapitiriza kutumikira Mulungu. Anapanga ciwembu cina. Yobu anadwala. Mkazi wa Yobu anaganiza kuti kucitira Mulungu mwano ndiko kwabwino koposa. Yobu sanafune kucita tero. Anakhulupirirabe Mulungu.

**18 May – Anzake a Yobu**

Werengani Yobu 2.11-13

Anzake a Yobu anamva cisoni. Atapita masiku ena anakambirana ngati Yobu alangidwa cifukwa ca chimo (Yobu 3-37). Yobu sanacimwe. M'masauso tiyenera kukhulupirira Mulungu pa nzeru zake.


**19 May – Kulemeranso**

Werengani Yobu 42.10-17

Mulungu anaciritsa Yobu. Yobu analinso wolemera. Analandira ana 10. Zitapita zaka zambiri Yobu anafa. Anapita Kumwamba. Kumwamba ndi malo abwino odabwitsa. Kodi mudzapita Kumwamba mukafa?

# Pemphero

## Pempherani kosaleka – 1 Atesaloniki 5.17a



**20 May – Kodi kupemphera ndiko ciani?**

<u>Werengani Salimo 62.1-8</u>

Sabata latha tinamva za Yobu. Yobu analankhula ndi Mulungu. Kulankhula ndi Mulungu ndiko kupemphera. Tikapemphera Mulungu atimva. M'Baibulo tiwerenga kuti kupemphera ndi kofunikira.

Lero tawerenga za kupemphera m'Salimo 62.8. Kupemphera ndiko kutsanulira mitima yathu pa maso pa Mulungu. Ganizirani cibekete cimene ciri ndi madzi mkati. Tikasondotsa cibekete madzi atayikira. Tikapemphera titayikira mitima yathu pa maso pa Mulungu. Timuuza zonse zimene tiganiza ndi kumva. Mulungu afuna kuti timuuze zimene zitikhudza. Tiyenera kumuuzanso pa zimene tiri acisoni ndiponso pa zimene tifuna kumuyamikira.

**Funso: Kodi kupemphera kutanthauzanji kwa inu?**

**21 May – Pempherani modzicepetsa**

Werengani Mlaliki 5.2

Mulungu ali Kumwamba. Afuna kumva zimene tikamba. Tikalankhula naye tiyenera kudzicepetsa. Zimene tikamba ziyenera kucokera m'mitima yathu.

**22 May – Kupemphera m'njira yotani**

Werengani Mateyu 6.5-6

Anthu ena akapemphera amalankhula ziganizo zabwino. Ena amalankhula mokweza. Nthawi zambiri afuna kulemekezedwa ndi anthu ena pa pemphero lao lamphamvu. Mulungu sayang'anira pemphero labwino loposa koma mitima yathu.

**23 May – Kupemphera m'dzina la Yesu**

Werengani Yohane 14.13 ndi 14

Ndife ocimwa. Sitiyenera kuyankhidwa titapemphera. Koma Mulungu anapanga njira yoyankhiramo mapemphero athu. Ayankha mapemphero cifukwa ca Yesu. Cifukwa ca ici tiyenera kupemphera m'dzina la Yesu.

**24 May – Pemphero losayankhidwa**

Werengani 2 Akorinto 12.7-10

Nthawi zambiri Paulo anapemphera thandizo. Mulungu sanacite zimene Paulo anafunsa. Nthawi zina Mulungu sacita zimene tifuna. Nthawi zina ali ndi maganizo abwino uposa maganizo athu. Tiyenera kumukhulupirira kuti adziwa zabwino zoposa za ife.

**25 May – Kupemphera ciani**

Werengani Mateyu 6.9-13

Yesu anapatsa citsanzo ca pemphero. Pempherolo lichedwa *Pemphero la Ambuye.* Tikapemphera tiyenera kulemekeza Mulungu, kuulula zolakwa zathu, kupemphera cimene tifunika komanso kupempherera anthu ena.

**26 May – Thandizo la Mulungu m'kupemphera**

Werengani Aroma 8.26

Ngati sitidziwa kupemphera, tifunse Mulungu. Baibulo litiphunzitsa kuti Mzimu Woyera afuna kutitsogolera.

# Samueli anatumikira Mulungu

Cifukwa cace, abale anga okondedwa, khalani okhazikika, osasunthika, akucuruka mu nchito ya Ambuye, nthawi zonse – 1 Akorinto 15.58a

**27 May – Kubadwa kwa Samueli**


<u>Werengani 1 Samuel 1.1-20</u>

Aisrayeli anakhala m'Kanani zaka zambiri. Mmodzi wa iwo ndiye Elikana. Anakwatira Hana ndi Penina. Penina anali ndi ana, koma Hana analibe. Penina anabvutitsa Hana posakhala ndi mwana.

Caka ciriconse iwo onse ankapita ku Silo kumene Cihema cinaliko. Cihema cinali hema lapadera kumene anthu anapembedza Mulungu ndi kumupereka nsembe.

Hana anamva cisoni kwambiri posakhala ndi mwana. Anapemphera Mulungu. Analonjeza kuti mwana wake adzatumikira Mulungu m'Cihema. Kunalibe munthu amene anamva mau ake, koma Mulungu anamumva. Mulungu anayankha pemphero lake. Hana analandira mwana. Dzina lake ndi Samueli. Samueli anatumikira Mulungu kucokera ku nthawi ya umwana wake.

**Funso: Kodi mudziwa zitsanzo za m'umoyo wanu kuti Mulungu ayankha mapemphero?**



**28 May – Hana anacita cimene adalonjeza**

Werengani 1 Samueli 1.24-28

Atamulera nthawi yaing'ono Hana anabweretsa Samueli ku Cihema. Kucokera ku nthawi iyo iye anali pamodzi ndi Eli, mkulu wansembe. Hana anacita zimene adalonjeza. Kodi mumacita zimene munalonjeza?

**29 May – Mulungu anaitana Samueli**

Werengani 1 Samueli 3.1-10

Masiku onse Samueli anathandiza Eli mkulu wansembe. Mwa kucita tero anamvera Mulungu. Anakonda Mulungu. Anali ndi zaka zocepa, komabe anatumikira Mulungu.

**30 May – Mulungu analankhula ndi Samueli**

Werengani 1 Samuel 3.11-19

Usiku Mulungu analankhula ndi Samueli. Anati kuti adzalanga banja la Eli cifukwa ana a amuna ake sanamvere Mulungu. Masiku ano Mulungu amalankhula ndi ife m'Baibulo.

**31 May – Eli anamwalira**

Werengani 1 Samueli 4.1-18

Mulungu analanga banja la Eli cifukwa ca macimo ao. Tikacimwa tinyoza Mulungu.

**1 June – Samueli anaphunzitsa Aisrayeli**

Werengani 1 Samueli 7.3-13

Aisrayeli sanamvere Mulungu. Anapembedza mafano. Mulungu anawalanga. Afilisti anawalamulira. Samueli anaphunzitsa Aisrayeli za kulapa. Aisrayeli anayenera kutumikira mafano ndiponso kupempha Mulungu cikhululukiro.

**2 June – Aisrayeli anafuna mfumu**

Werengani 1 Samueli 8.4-10

Aisrayeli anafuna mfumu. Mulungu ndiye Mfumu wao, koma anafuna mfumu monga mitundu ina anakhala nayo. Mulungu anawacenjeza kuti mfumu idzakhala mfumu yoipa (1 Samueli 8.11-18). Aisrayeli sanamumvere.

# Mfumu Sauli

Wosunga mwambo ali m'njira ya moyo; Koma wosiya cidzudzulo asocera – Miyambi 10.17


**3 June – Sauli anadzodzedwa**

Werengani 1 Samueli 9.17-27 ndi 1 Samueli 10.1

Mulungu anauza mneneri Samueli kuti Sauli adzakhala mfumu watsopano. Tsiku lina Sauli ndi mneneri Samueli anakomana. Mneneri Samueli anauza Sauli kuti adzakhala mfumu wa Israyeli. Sauli anadabwa. Iye ndiye munthu wamba cabe. Sanamvetse ndi cifukwa ciani Mulungu anamsankha. Sauli anadzicepetsa. Mulungu afuna anthu kukhala odzicepetsa.

Mneneri Samueli anatenga mafuta. Anawaika pa mutu wa Sauli. Ico cinali cizindikiro kuti Sauli adzakhala mfumu.

**Funso: Kodi ndinu munthu wodzicepetsa?**



**4 June – Sauli anasankhidwa kukhala mfumu**

Werengani 1 Samueli 10.17-25

Mneneri Samueli anauza Aisrayeli kuti Mulungu afuna Sauli kukhala mfumu wao. Aisrayeli akaona Sauli anakondwera kwambiri.

**5 June – Nkhondo**

Werengani 1 Samueli 11.1-11

Mfumu Sauli ndi ankhondo ake anathandiza anthu a ku Yabezi. Mfumu Sauli anali mfumu wabwino ndi wolimba mtima. Anacita zimene Mulungu afuna.

**6 June – Kusamvera kwa mfumu Sauli**

Werengani 1 Samueli 13.8-14

Mneneri Samueli analonjeza kubwera kuti apereke nsembe kwa Mulungu nakumpempha thandizo. Mfumu Sauli sanafune kuyembekezera kufika kwa mneneri Samueli. Anapereka nsembe. Ico cinali chimo. Mulungu adzasankha mfumu watsopano.

**7 June – Kusamveranso**

Werengani 1 Samueli 15.1-9

Mulungu anauza mfumu Sauli kuti ayenera kupha Aamaleki onse. Anayenera kutentha akatundu ao onse. Mfumu Sauli sanamvere. Sanaphe onse. Sanatenthe zonse. Kodi mumamvera Mulungu nthawi zonse?

**8 June – Mfumu woipa**

Werengani 1 Samueli 15.10-23

Mneneri Samueli anauza mfumu Sauli kuti anacita zoipa. Mulungu sanakondwere ndi mfumu Sauli. Sauli sanadzicepetsebe. Mfumu Sauli sanakonde Mulungu ndipo sanatumikire Mulungu ndi mtima wake.


**9 June – Mneneri Samueli anadzodza Davide**

Werengani 1 Samueli 16.1-13

Mfumu Sauli anali mfumu woipa. Mulungu anafuna Davide kukhala mfumu. Mulungu anamusankha cifukwa mtima wake unali wabwino pa maso pake. Mulungu ayang’ana mitima yathu. Mneneri Samueli anadzodza Davide. Davide adzakhala mfumu.

# Davide anasanduka mfumu

Iye anakuuza, munthuwe, comwe ciri cokoma; ndipo Yehova afunanji nawe koma kuti ucite colungama, ndi kukonda cifundo ndi kuyenda modzicepetsa ndi Mulungu wako? – Mika 6.8b



**10 June – Davide ndi Goliati**

Werengani 1 Samueli 17.21-26 ndi 17.40-51

Afilisti anamenyana ndi Aisrayeli. Mmodzi wa iwo ndiye Goliati. Anali munthu wamtali kwambiri ndi wamphamvu. Goliati anadzikweza. Goliati ananyenga Mulungu ndi Aisrayeli. Ico ndi chimo.

Davide atamva Goliati wonyoza Mulungu anamva cisoni. Davide anakonda Mulungu. Anafuna kumenyana Goliati. Mulungu anamuthandiza. Goliati anafa. Anthu onse anaona kuti Mulungu ndi wamphamvu yonse.

**Funso: Kodi mukumva bwanji mukamva kuti anthu ena anyoza Mulungu?**

**11 June – Davide anayenera kuthawa**

Werengani 1 Samueli 18.28-30 ndi 19.1-10

Mfumu Sauli anada Davide cifukwa anthu anakonda Davide kuposa mfumu Sauli. Mfumu Sauli acita kaduka. Nsanje ndi chimo. Mfumu Sauli anafuna kupha Davide. Davide anayenera kuthawa.

**12 June – Davide anakondabe mfumu Sauli**

Werengani 1 Samuel 24.1-10 ndi 24.16-22

Mfumu Sauli sanali wokoma mtima kwa Davide. Koma Davide anali wokoma mtima kwa iye. Sanaphe mfumu Sauli. Mulungu afuna kuti tikonda adani athu.

**13 June – Mfumu Sauli anamwalira**

Werengani 2 Samueli 1.1-12

Mfumu Sauli anafa. Davide anamva cisoni kwambiri, ngakhale anali mdani wake. Davide anakhala mfumu watsopano, monga Mulungu adalonjeza kale. Mulungu ndiye Mfumu wa Mafumu. Kodi mupempha Mulungu kukhalenso Mfumu wa umoyo wanu?

**14 June – Mfumu Davide ndi Mefiboseti**

Werengani 2 Samueli 9

Mefiboseti anaitanidwa kubwera kwa mfumu Davide. Anamva mantha, koma mfumu anali wokoma mtima kwa iye. Mfumu Davide anali mfumu wabwino. Yesu ndiyenso Mfumu wabwino. Afuna kupulumutsa ndi kulamulira anthu ocimwa.

**15 June – Mfumu Davide anacimwa**

Werengani 2 Samueli 11.1-5 ndi 11.14-17

Mfumu Davide anacita cigololo ndi Bateseba. Sanafune munthu wina aliyense kudziwa cimene anacita. Ndiye anafuna kuti mwamuna wa Bateseba afe. Mfumu Davide anacimwa. Ndi cacisoni kwambiri!

**16 June – Kupempherera cikhululukiro**

Werengani 2 Samueli 12.7-14

Mneneri Natani anauza mfumu Davide kuti adacimwa. Davide anamva cisoni. Anapempha cikhululukiro. Tiyenera kumvanso cisoni pa macimo athu ndi kupempha cikhululukiro ca macimo athu.

# Pemphero la mfumu Davide

## Mundicitire ine cifundo, Mulungu – Salimo 51.1a

**17 June – Mfumu Davide analapa**

<u>Werengani Salimo 51.1 and 2</u>

Sabata latha tinamva kuti mfumu Davide anacimwa. Anacita cigololo ndi Bateseba. Anafuna kuti mwamuna wa Bateseba afe. Davide anamva cisoni pa zimene adacita. Analemba nyimbo. Nyimboyo ndi Salimo 51. M'Salimo 51 tiwerenga zimene Davide ananena kwa Mulungu.

Davide anapempha cifundo. Anati kuti adziwa Mulungu ndiye wacifundo. Anapempha Mulungu kumucitirenso cifundo. Anadziwa kuti yankho lenileni la chimo lake ndilo kulandira cikhululukiro.

**Funso: Kodi mumapemphera ciani mutacimwa?**



**18 June – Kuulula macimo**

Werengani Salimo 51.3 ndi 4

Mfumu Davide anazindikira kuti adacita zoipa. Anacimwira Mulungu. Analephera kucita zimene Mulungu afuna. Anadziwa kuti ayenera kulangidwa cifukwa ca macimo ake. Ciweruzo ca Mulungu ndico coona. Kodi mumaulula macimo anu?

**19 June – Ciyambi ca uchimo**

Werengani Salimo 51.5

Mfumu Davide anati kuti mtima wake ndi wocimwa. Ali ndi uchimo nthawi zonse. gakhale asanabadwe mtima wake sunali wolungama pa maso pa Mulungu. Mfumu Davide anadziwa kuti ndiye wocimwa ndithu.

**20 June – Zimene Mulungu afuna**

Werengani Salimo 51.6

Mulungu afuna anthu kukhala olungama pa maso pake. Mulungu afuna kuti anthu akhale anzeru. Davide analakwadi. Kodi mwalakwanso?

**21 June – Zimene mfumu Davide anapempha**

Werengani Salimo 51.7-11

Mfumu Davide anadziwa kuti Mulungu angamusiye cifukwa ca chimo lake. Davide anapempha Mulungu kuti asamusiye. Anadziwa kuti kopanda Mulungu iye ndiye wotayika. Kodi mungamve bwanji ngati Mulungu akusiyani cifukwa ca macimo anu?

**22 June – Lonjezo**

Werengani Salimo 51.12-15

Mfumu Davide anapempha Mulungu kuti akhale naye. Mwa thandizo la Mulungu angaphunzitse anthu ena za Mulungu. Angalemekeze Mulungu pa cisomo cake.

**23 June – Kumvera Mulungu moonadi**

Werengani Salimo 51.16-19

M’cipangano cakale anthu ankapereka Mulungu nsembe. Ico cinali njira yopempha cikhululukiro. Mfumu Davide anadziwa kuti Mulungu sakondwera ndi nsembe cabe. Mulungu afuna anthu kumutumikira ndi mitima yao.

# Mfumu Solomo

Kumuopa Yehova ndiko ciyambi ca nzeru; Onse akucita cotero ali naco cidziwitso cokoma – Psalm 111.10a



**24 June – Mfumu watsopano**

Werengani 1 Mafumu 1.28-40

Mfumu Davide anakalamba. Anafuna mwana wa mwamuna wake Solomo kukhala mfumu. Mfumu Davide anauza mkazi wake Bateseba kuti Solomo ayenera kukhala mfumu watsopano. Bateseba anabvomereza.

Mfumu Davide anaitana  Zadoki wansembe, Natani mneneri ndi Benaya. Anawauza kuti ayenera kudzodza Solomo kukhala mfumu. Anabvomerezanso. Zadoki wansembe anadzodza Solomo. Ico cinali cizindikiro kuti Mulungu afuna Solomo kukhala mfumu watsopano. Anthu onse anamva kuti Solomo ndiye mfumu watsopano. Anakondwera kwambiri ndi mfumu wao.

**Funso: Kodi mumapempherera otilamulira?**

**25 June – Funso la Mulungu**

Werengani 1 Mafumu 3.5-15

Solomo anapempha Mulungu nzeru kuti alamulire bwino. Chuma ndi ulemu sizinali zofunikira zoposa kwa iye. Mulungu analonjeza kumupatsa nzeru. Nanga inu, mungapemphe ciani kwa Mulungu?

**26 June – Mfumu wanzeru**

Werengani 1 Mafumu 3.16-28

Mfumu Solomo anayenera kudziwa kuti mai wake wa mwana ndiye yani. Anacita monga anafuna kupha ndi kugawa mwana. Mkazi umodzi sanafune tero. Mfumu Solomo anadziwa kuti mkaziyo ndiye mai wa mwana. Mfumu Solomo anali wanzeru kwambiri.

**27 June – Kacisi wa Mulungu**

Werengani 1 Mafumu 5.2-5 ndi 6.11-14

Mfumu Solomo anamanga Kacisi wa Mulungu. M'Kacisi anthu ankapemphera Mulungu. Ankapereka nsembe kupempha cikhululukiro ndi kuyamika Mulungu. Mulungu anati Aisrayeli azimumvera nthawi zonse.

**28 June – Mfumu yaikazi ya dziko lakutali**

Werengani 1 Mafumu 10.1-13

Mfumu yaikazi ya dziko lakutali anabwera kwa mfumu Solomo. Analankhula naye. Anati kuti mfumu Solomo anali wanzeru kuposa maganizo ake. Mulungu ndiye wanzeru kuposa Solomo. Salephera kutithandiza nthawi zonse.

**29 June – Mafano**

Werengani 1 Mafumu 11.1-8

Mfumu Solomo anali ndi akazi ambiri. Akaziwo sanapembedze Mulungu. Anapembedza mafano. Mfumu Solomo anayamba kupembedza mafano. Ndi coipa kwambiri!


**30 June – Cilango ca Mulungu**

Werengani 1 Mafumu 11.9-13

Mulungu anakwiya ndi mfumu Solomo. Cinthu coipa cidzacitika atamwalira Solomo. Mwana wa mwamuna wake adzalamulira mbali yaing'ono ya dziko. Mbali ina idzalamuliridwa ndi munthu wina. Mbali ina yochedwa Yuda, mbali ina Israyeli.

# Ziphunzitso za mneneri Eliya

Ine ndidzakulangiza ndi kuphunzitsa iwe za njira ukayendayo;
Ndidzakupangira ndi diso langa lakuyang'ana iwe – Salimo 32.8



**1 July – Cilango ca Mulungu cifukwa ca kupembedza mafano**

Werengani 1 Mafumu 17.1-6

Mfumu Solomo adafa. Pa nthawi ya mneneri Eliya, mfumu Ahabu analamulira. Mfumu Ahabu sanakonde Mulungu ndipo sanamumvere. Anapanga fano. Dzina la fanolo ndi Baala. Mfumu anauza anthu kupembedza Baala m'malo mwa Mulungu. Fano ndilo kalikonse komwe ndi kofunikira kwa ife kuposa Mulungu.

Mneneri Eliya ndi anthu ena sanafune kupembedza Baala. Anafuna kupembedza Mulungu yekha. Mneneri Eliya anapita kwa mfumu Ahabu ndi uthenga wa Mulungu. Cifukwa ca ico Eliya achedwa mneneri. Anauza anthu uthenga wa Mulungu.

Mneneri Eliya anati kwa mfumu Ahabu kuti sikudzakhala mvula nthawi yaitali. Kudzauma. Ico cinali cilango ca Mulungu cifukwa ca macimo omwe anthu anacita.

Mfumu Ahabu anakalipa kwambiri ndi Eliya cifukwa ca cilango. Mneneri Eliya anapita  ku mapiri kukabisala mfumu. Mulungu anamusamalira kumeneko.

**Funso: Kodi mumayankha bwanji ziphunzitso za Mulungu m'Baibulo?**

**2 July – M'nyumba ya mkazi wa masiye**

Werengani 1 Mafumu 17.7-16

Mneneri Eliya anapempha mkazi wa masiye kuti amupatse madzi ndi cakudya. Analibe cakudya cokwanira. Anakhulupirira kuti Mulungu adzapatsa zimene afunika. Mulungu anasamalira iwo onse.

**3 July – Mwana wa mkazi wa masiye**

Werengani 1 Mafumu 17.17-24

Mulungu anagwiritsa nchito Eliya kuukitsa mwana kwa akufa. Baibulo likamba kuti anthu ocimwa ndiwo akufa m'mzimu, cifukwa mitima yao ndi yocimwa. Tifunika kulandira moyo wa uzimu kwa Mulungu. Baibulo likamba kuti ici ndi 'kubadwa mwatsopano'.

**4 July – Ku phiri la Karimeli**

Werengani 1 Mafumu 18.17-21

Mneneri Eliya anauza anthu opembedza Baala kubwera ku Phiri la Karimeli. Anati kuti ayenera kusankha kutumikira Mulungu kapena kutumikira mafano. Kodi mumasankha ciani mwa izi ziwiri?

**5 July – Mulungu anayankha**

Werengani 1 Mafumu 18.22-40

Baala sanayankhe aneneri ake. Baala si ndiye mulungu. Saliko. Mulungu anayankha pemphero la mneneri Eliya. Mulungu yekha ndiye Mulungu woonadi.

**6 July – Mulungu anapatsa mvula**

Werengani 1 Mafumu 18.41-46

Patapita nthawi ya cilala Mulungu anapatsa Aisrayeli mvula. Sanaiyenere. Mulungu ndi wacisomo. Iye yekha ndiye Mulungu.

**7 July – Mulungu ali cimodzi-modzi**

Werengani 2 Mafumu 2.9-14

Mulungu ananyamula mneneri Eliya Kumwamba modabwitsa. Elisa anali mneneri watsopano. Mulungu anathandiza mneneri Elisa m'njira imodzimodzi monga adathandiza mneneri Eliya. Mulungu sasintha nthawi zonse.

# Mulungu anasamalira mneneri Elisa

Ndipo onse akufuna kukhala opembedza m'moyo mwa Kristu Yesu, adzamva mazunzo – 1 Timoteo 3.12



**8 July – Zimbalangondo ziwiri**

Werengani 2 Mafumu 2.23 ndi 24

Mneneri Elisa anali mtumiki wa Mulungu. Anayenera kuphunzitsa Aisrayeli za Mulungu.

Tsiku lina mneneri Elisa anapita ku Beteli. Anyamata ang'ono anaona mneneri Elisa pobwera. Sanakondwere kuti apita ku Beteli. Sanafune kumvera mneneri Elisa. Sanafune kumva za Mulungu. Anyamata ananyoza Elisa. Mwa kunyoza mtumiki wa Mulungu ananyoza Mulungu yemwe. Mneneri Elisa anawauza kuti acita coipa. Mwadzidzidzi zimbalangondo (zilombo zazikulu zoopsa) ziwiri zinaturuka kuthengo. Zinapha anyamata ambiri. Tiyenera kumva zimene Mulungu afuna kutiuza.

**Funso: Kodi mumamva mosamalira pamene Mulungu alankhula nanu m'Baibulo?**

**9 July – Namani anaciritsidwa**

Werengani 2 Mafumu 5.1-14

Namani anapita ku Israyeli kuti aciritsidwe. Mfumu wa Israyeli sanakhoze kumuciritsa. Mulungu yekha akhoza kuciritsa. Namani anapita kwa mneneri Elisa. Poyamba sanakhulupirire mneneri Elisa. Kenaka anakasamba m'mtsinje. Anaciritsidwa.

**10 July – Cisamaliro ca Mulungu**

Werengani 2 Mafumu 6.8-10

Mfumu wa Aramu anamenyana ndi Aisrayeli. Koma mneneri Elisa anauza mfumu ya Israyeli nthawi yoponya nkhondo ndiponso malo ake. Mulungu adziwa zonse. Amathandiza anthu ake. Kodi ndinu mmodzi wa anthu ake?

**11 July – Citetezo ca Mulungu**

Werengani 2 Mafumu 6.11-17

Mfumu wa Aramu anakalipa ndi mneneri Elisa. Anatuma asirikali ake kumugwira. Mneneri Elisa sanaope. Anadziwa kuti Mulungu adza muteteza. Ngati ndinu mwana wa Mulungu simuyenera kuopa kalikonse.

**12 July – Adani m'Samariya**

Werengani 2 Mafumu 6.18-20

Mulungu anacititsa khungu asirikali kuti sanadzindikire Elisa. Mneneri Elisa anawapereka ku Samariya. Asirikali anagwiridwa. Mulungu anasamalira mtumiki wake.

**13 July – Kusamalira adani**

Werengani 2 Mafumu 6.21-23

Mneneri Elisa anali wokoma mtima kwa adani. Adani anapatsidwa cakudya. Anamasulidwa. Mulungu ndiyenso wokoma mtima kwa adani ake. Afuna anthu ocimwa alape ndi kukhala anthu ake. Kodi muyenera kulapa kwa ciani lero?

**14 July – Imfa ya Elisa**

Werengani 2 Mafumu 13.14-20

Kumenyana ndi Aramu kunapitiriza. Mfumu ya Israyeli anadziwa kuti adzapambana cabe ngati Mulungu ali nao. Asanamwalire Elisa, Mulungu analonjeza kuti adzapitiriza kuthandiza Aisrayeli. Tifunika thandizo la Mulungu nthawi zonse.

# Mfumu Hezekiya

Tsiku la msauko wanga ndidzaitani Inu; Popeza mudzandibvomereza – Salimo 86.7



**15 July – Citsanzo cabwino**

Werengani 2 Mafumu 18.1-7

Mfumu Hezekiya ankacita zimene zinali zabwino pa maso pa Mulungu. Mfumu Hezekiya anamvera Mulungu. Mfumu Hezekiya anaononga mafano onse. Sanalole anthu kupembedza mafano. Anakhulupirira Mulungu m'zonse zimene anacita. Anadziwa kuti afunika Mulungu. Kopanda Mulungu sanakwaniritse kulamulira bwino.

Baibulo likamba kuti Mulungu anali pafupi ndi mfumu Hezekiya. Mfumu Hezekiya anali citsanzo cabwino ca anthu m'mene ayenera kutumikira Mulungu.

**Funso: Kodi ndinu citsanzo ca yani ca kutumikira Mulungu?**

**16 July – M'mabvuto**

Werengani 2 Mafumu 18.13 ndi 28-35

Mfumu Hezekiya ndi anthu ake anabvutika. Aasuri anadza kucita nao ukhondo. Kazembe anati kuti kudalira pa thandizo la Mulungu sikudzawathandiza. Anati kuti Mulungu sadzawapulumutsa.

**17 July – Kupempherera thandizo**

Werengani 2 Mafumu 19.1-4

Mfumu Hezekiya anamva zimene zidacitika. Anamva cisoni. Anapita ku Kacisi kukapemphera. Anatuma anthu kupita kwa Yesaya, mneneri wa Mulungu. Anthuwo anapempha mneneri Yesaya kuti apempherenso. Kodi mumapempherera anthu obvutika?

**18 July – Lonjezo la Mulungu**

Werengani 2 Mafumu 19.5 and 6

Mneneri Yesaya anati kuti Mulungu adzapulumutsa anthu. Sanayenere kuopa.

**19 July – Kalata**

Werengani 2 Mafumu 19.14-19

Mfumu Hezekiya analandira kalata la Aasuri. M'kalata munalembedwa kuti Mulungu sadzawapulumutsa. Mfumu Hezekiya anapempha thandizo la Mulungu. Anapempha Mulungu kuonetsa kuti Iye yekha ndiye Mulungu woonadi.

**20 July – Mulungu anayankha**

Werengani 2 Mafumu 19.35-37

Mulungu anacita zimene adalonjeza. Aasuri ambiri anaphedwa ndi Iye. Mfumu ya Aasuri inadzindikira kuti Mulungu ndi wamphamvu kuposa iwo.

**21 July – Mfumu Hezekiya anadwala**

Werengani 2 Mafumu 20.1-7

Mulungu anauza mfumu Hezekiya kuti adzafa. Mfumu Hezekiya anapempha Mulungu kumuciritsa. Mulungu anayankha pemphero lake. Patapita masiku atatu anapita ku Kacisi kukayamikira Mulungu. Kodi muyamikira Mulungu pamene akuciritsani?

# Umoyo wa Yona

## Yehova ngwa cifundo ndi wolungama – Salimo 116.5a

**22 July – Kusamvera kwa Yona**

Werengani Jonah 1.1-3

Mulungu adziwa zonse. Anadziwa kuti anthu a ku Nineve sanamumvere. Anthu anamulemetsa. Mulungu anatuma Yona ku Nineve kuti akalalike. Yona anacita mwano. Kukana kucita cifuniro ca Mulungu ndiko chimo. Yona anaganiza kuti angazembe Mulungu.

**Funso: Kodi kuli kusamvera kwa Mulungu m'umoyo wanu?**



**23 July – Namondwe**

Werengani Yona 1.4-10

Mulungu anautsa cimphepo cacikulu. Anacita tero cifukwa ca kusamvera kwa Yona. Anthu m'combo anaopa kuti angafe. Nthawi zina mabvuto m'miyoyo yathu ndiyo otsatira a macimo athu.

**24 July – Yona m'nyanja**

Werengani Yona 1.11-17

Yona anaponyedwa m'nyanja. Kunali bata. Yona anayenera kutha psiti m'nyanja cifukwa ca kusamvera kwake. Koma Mulungu anali wacifundo. Anatuma cinsomba cimene cinameza Yona.

**25 July – Pemphero la Yona**

Werengani Yona 2

Yona anadziwa kuti adacita zoipa. Anapempha Mulungu cikhululukiro. Cinsomba cinamusanzira ku mtunda. Yona anapulumuka cifukwa ca cisomo ca Mulungu.

**26 July – Yona analalikira m'Nineve**

Werengani Yona 3.1-4

Mulungu anatumanso Yona ku Nineve. Yona anamvera. Anauza anthu uthenga wa Mulungu. Patapita masiku 40 mzinda wa Nineve udzaonongedwa. Nthawi zonse anthu a Mulungu ayenera kunena zimene Mulungu awauza.

**27 July – Anthu a ku Nineve analapa**

Werengani Yona 3.5-10

Anthu a ku Nineve anadziwa kuti ayenera kulangidwa cifukwa ca macimo ao. Analapa: analeka kucita zoipa ndipo anapemphera cikhululukiro. Mulungu sanawalange.

**28 July – Mulungu ndiye wacisomo**

Werengani Yona 4

Yona anafuna kuti mtengo upulumuke, koma kuti anthu asapulumuke. Yona sanali wokoma mtima kwa anthu a ku Nineve. Mulungu ndiye wacisomo woposa anthu onse.

# Danieli ndi anzake

Tiyenera kumvera Mulungu koposa anthu – Macitidwe a Atumwi 5.29b

**29 July – Kubweretsedwa ku Babulo**

<u>Werengani Danieli 1.1-8</u>

Mafumu ambiri adalamulira dziko. Anthu anapembedzabe mafano. Mulungu anawalanga. Mfumu wa Babulo, Nebukadinezara, anaononga dziko lao.

Danieli ndi anzake anatengedwa kapolo nabweretsedwa ku Babulo. Mfumu anafuna kuti iwo akhale anzeru. Anawasamalira bwino. Iwo anapatsidwa cakudya cokoma ndi zakumwa zokoma.

Danieli anadziwa kuti cakudya copatsidwa ndi zakumwa zopatsidwa zidaperekedwa nsembe ku mafano. Sanafune kudya cakudya ico kapena kumwa zakumwa izo. Sanafune kucimwa.

**Funso: Kodi mumacita ciani pamene anthu ena afuna kukucimwitsani?**



**30 July – Kukhala anzeru uposa anthu ena**

Werengani Danieli 1.9-20

Danieli ndi anzake anapempha madzi, mkate ndi zina zomera m'nthaka. Cakudya ico sicinaperekedwa nsembe ku mafano. Mulungu anawadalitsa pomumvera. Iwo anali athanzi ndi anzeru uposa ena onse.

**31 July – Fano la mfumu**

Werengani Danieli 3.1-7

Mfumu Nebukadinezara anapanga fano lalikulu la golide. Anafuna anthu onse kulipembedza. Anati kuti munthu aliyense yemwe samumvera adzaponyedwa m'moto.

**1 August – Kukana kugwada**

Werengani Danieli 3.8-18

Anzake atatu a Danieli anakana kupembedza fano. Kukana kunali koopsa: angafe m'moto. Koma anakonda Mulungu kuposa wina aliyense.

**2 August – Kutetezedwa m'moto**

Werengani Danieli 3.19-30

Mfumu anakalipa ndi anzake a Danieli. Iwo anaponyedwa m'moto. Koma Mulungu anakhala nao. Sanafe. Tiyenera kupempha Mulungu thandizo lake kuti tizimumvera nthawi zonse.

**3 August – Danieli pa cipsezo**

Werengani Danieli 6.1-18

Danieli anali mtumiki wa Dariyo, mfumu watsopano. Atumiki ena anamucita kaduka Danieli. Anafuna kuti Danieli afe. Anapanga lamulo latsopano. Kunalibe munthu amene aloledwa kupemphera kwa Mulungu. Danieli anapitiriza kupemphera.


**4 August – Mulungu anatetezera Danieli**

Werengani Danieli 6.19-24

Mulungu anateteza Danieli ku mikango. Mulungu anaonetsa kuti Iye yekha ndiye Mulungu woona. Mfumu anauza anthu onse kumvera Mulungu yekha. Mulungu afuna kuti tizikana kucimwa.

# Yesu analonjezedwa

## Kondwera kwambiri (...) Mfumu yako ikudza kwa iwe; ndiye wolungama, ndi Mwini cipulumutso – Zekariya 9.9a



**5 August – Maina a Yesu**

Werengani Yesaya 9.6

Tinaphunzira kale kuti m'Baibulo muli zigawo ziwiri. M'cigawo coyamba (ndico cipangano cakale) Mwana wa Mulungu, Yesu Kristu, analonjezedwa pobadwa pa dziko lapansi. Sabata iri tidzaphunzira malonjezo awa ena. Yesaya anali mneneri. Anaphunzitsa anthu zambiri za Mulungu. Anawauza kuti Yesu adzabwera kukapulumutsa anthu ocimwa. M'Yesaya 9.6 tawerenga maina osiyanasiyana omwe mneneri Yesaya anapatsa kwa Yesu. Maina awa atiphunzitsa za Yesu.

*Wodabwitsa*. Yesu ndiye Mwana wa Mulungu. Anadza pa dziko lapansi. Anacita zodabwitsa. Mwa imfa yake ya pa mtanda anakhululukira macimo a anthu ake. *Wauphungu.* Yesu anaphunzitsa za Mulungu. Yesu ndiye wanzeru. Tiloledwa kumupempha thandizo nthawi zonse. *Mulungu wamphamvu.* Yesu anacita zimene siziri zothekha kwa ife. Anadza kubweretsanso ocimwa kwa Mulungu. *Atate Wosatha.* Yesu ndiye Mulungu. Anakhalako nthawi zonse ndipo adzakhalako nthawi zonse. *Kalonga wa mtendere.* Yesu yekha ndiye Mkhalapakati yemwe abwezerenso ubwenzi pakati pa Mulungu ndi anthu. Mwa Yesu tikhale ndi mtendere ndi Mulungu.

**Funso: Kodi maina a Yesu atanthauza ciani kwa inu?**

**6 August – Nthambi**

Werengani Yesaya 11.1 ndi 2

Aisrayeli anali monga mtengo wodulika: obalalika ndi osafunikira. Mneneri Yesaya anati kuti Yesu adzakhala monga nthambi ikula m'mtengo wodulika. Yesu adzabadwa. Adzakhala Mfumu.

**7 August – Dzuwa**

Werengani Malakai 4.2

Yesu achedwa Dzuwa. Kucokera ku nthawi ya uchimo m'Paradaiso kulibe cimwemwe ceniceni koma mdima wauzimu. Yesu ndiye Dzuwa. Apatsa cimwemwe ceniceni. Anthu amene ali ake ndiwo okondweradi.

**8 August – Imanueli**

Werengani Yesaya 7.14

Mneneri Yesaya anati kuti Yesu adzabadwa mwa namwali. Dzina lina la Yesu ndi Imanueli. Dzinalo litanthauza 'Mulungu nafe'. Mulungu ndi anthu akhale pamodzi cifukwa ca Yesu. Yesu anacotsera mkwiyo wa Mulungu wa uchimo wa anthu ake.

**9 August – Kubadwa m'Betelehemu**

Werengani Mika 5.2

Mneneri Mika anati kuti Yesu adzabadwa m'mzinda wopanda nchito: Betelehemu. Yesu afunafuna anthu opanda nchito kulingana ndi anthu ena. Yesu anadzicepetsa.

**10 August – Mfumu**

Werengani Yeremiya 23.5 ndi 6

Mneneri Yeremiya anati kuti Yesu adzabadwa m'banja la mfumu Davide. Adzakhala mfumu woona. Adzacita zimene ziri zolungama. Adzapulumutsa anthu ake ku macimo ao.

**11 August – Yesu adzazunzika**

Werengani Yesaya 52.13 ndi 14

Mneneri Yesaya ananena kuti Yesu adzakhala Mfumu. Komanso adzazunzika ndipo adzafa. Mwa kucita tero Iye ndiye Mfumu wa uchimo, imfa ndi Satana (Yesaya 53).

# Uthenga wa Mulungu wa kwa Zakariya ndi Mariya

Cifukwa palibe mau amodzi akucokera kwa Mulungu adzakhala opanda mphamvu – Luka 1.37

**12 August – Uthenga wa Mulungu wa kwa Zakariya**


Werengani Luka 1.5-17

Anthu ambiri m'cipangano cakale analakalaka kubadwa kwa Yesu. Anamva kuti ananyoza Mulungu pomucimwira. Anafunika Yesu kuti acotse macimo ao. Anafuna kuti Mulungu alemekezedwenso.

Zakariya ndi Elisabeti analakalakanso kubadwa kwa Yesu. Anakalamba ndipo analibe mwana. Zakariya anali wansembe m'Kacisi. Kacisi unali malo kumene anthu ankapereka nsembe napempha Mulungu cikhululukiro.

Tsiku lina mngelo anauza Zakariya kuti adzakhala ndi mwana: Yohane. Yohane adzakhala mtumiki wa Mulungu. Mwa ulaliki wake anthu ambiri adzazindikira kuti anafunika Yesu. Yesu adzabadwa mwacangu.

**Funso: Kodi mufunika Yesu kuti acotse macimo anu?**



**13 August – Yankho la Zakariya**

Werengani Luka 1.18-25

Zakariya sanakhulupirire kuti adzakhala ndi mwana. Koma ciriconse cimene Mulungu akamba cicitika. Kulibe ciriconse cimene si citheka kwa Mulungu. Nthawi zambiri tisowa cikhulupiriro. Tizipempha Mulungu kuti atipatse cikhulupiriro mwa Iye.

**14 August – Uthenga wa Mulungu wa kwa Mariya**

Werengani Luka 1.26-33

Mngelo Gabrieli anatumidwa kwa Mariya. Anamuuza kuti adzakhala ndi mwana: Ambuye Yesu. Ndiwo uthenga wodabwitsa!

**15 August – Yankho la Mariya**

Werengani Luka 1.34-38

Mariya sanakwatiwe. Anadabwa kuti adzakhala ndi mwana motani. Mngelo anafotokoza kuti Mulungu ndiye Tate wa Mwana. Yesu ndiye Mwana wa Mulungu. Mariya anafuna kuti kufuna kwa Mulungu kucitike.

**16 August – Mariya anapita kwa Elisabeti**

Werengani Luka 1.39-45

Mariya anapita kwa Elisabeti. Analankhulana za uthenga wa Mulungu wa kubadwa mwacangu kwa Yesu. Anakondwera. Kulankhula za Mulungu ndi anthu ena ndiko kwabwino.

**17 August – Nyimbo ya Mariya**

Werengani Luka 1.46-56

Mariya anaimba nyimbo yolemekeza Mulungu. Anakondweradi cifukwa ca uthenga wabwino. Kodi mumaimba nyimbo yolemekeza Mulungu?

**18 August – Kubadwa kwa Yohane**

Werengani Luka 1.57-66

Yohane, mwana wa Zakariya ndi Elisabeti, anabadwa. Anthu anazindikira kuti iye si ndiye mwana wamba. Yohane ndiye mtumiki wa Mulungu, monga mngelo adanenera.

# Kubadwa kwa Yesu Kristu

Ndipo adzabala Mwana wa mwamuna, ndipo udzamucha dzina lace Yesu; pakuti Iyeyo adzapulumutsa anthu ace ku macimo ao – Matthew 1.21

**19 August – Yesu anabadwa**


Werengani Luka 2.1-7

Yosefe ndi Mariya anapita ku Betelehemu. Ico ndi cimene Kaisara Augusto, wolamulira wa masiku awo, anafuna. Atafika ku Betelehemu anafuna malo ogonapo. Sanapeze malo. Ico cinali cokhumutsidwa. Mwana wa Mariya, Yesu, adzabadwa msanga. Anafunika malo okhalapo. Potsiriza Yosefe ndi Mariya anapeza malo okhalapo: khola. Yesu anabadwa momwemo. Yesu, Mwana wa Mulungu, anacokera Kumwamba nabadwa m'khola lodetsedwa. Yesu anadzicepetsa.

Mitima yathu ndi monga khola: ndiyo yakuda cifukwa ca uchimo. Komabe Yesu afuna kubadwa m'mitima yathu. Ici citanthauza kuti afuna kuiyeretsa mwa kucotsa uve wa uchimo. Afuna kukhala Mfumu wathu.

Ngati mudziwa kuti mtima wanu ndi umoyo wanu ndiwo wakuda monga khola, pemphani Yesu kukhala m'mtima wanu. Yesu yekha akwaniritsa kucotsa macimo anu a m'mtima wanu. Akhoza ndipo afuna kuuyeretsa.

**Funso: Kodi kubadwa kwa Yesu kutanthauza ciani kwa inu?**



**20 August – Abusa**

Werengani Luka 2.8-20

Angelo anauza abusa kuti Yesu adabadwa. Abusa anafalitsa uthenga wabwino kwa anthu onse. Kodi mumafalitsa uthenga wabwino wa Yesu?

**21 August – Simeoni m'Kacisi**

Werengani Luka 2.22-35

Yosefe ndi Mariya anapita ndi Yesu ku Kacisi. Anayamika Mulungu polandira Mwana. Simeoni analemekeza Mulungu cifukwa Mulungu anacita cimene adalonjeza.

**22 August – Anna m'Kacisi**

Werengani Luka 2.36-40

Anna analinso m'Kacisi. Masiku onse ankakhalako kupembedza Mulungu. Ataona Yesu anakondwera kwambiri. Yesu anali Mpulumutsi wake.

**23 August – Anzeru**

Werengani Mateyu 2.1-8

Amuna okhala m'dziko lakutali anaona nyenyezi yapadera. Anadziwa kuti Mfumu Yesu adabadwa. anayamba ulendo wao kukamupeza. Mfumu Herode sanapite kukamupeza. Nanga inu mungacite ciani?

**24 August – Anzeru anapeza Yesu**

Werengani Mateyu 2.9-12

Nyenyezi inaonetsa amuna malo pomwe apezapo Yesu. Tipeze Yesu mwa kuwerenga Baibulo.

**25 August – Mfumu Herode anapha ana**

Werengani Mateyu 2.13-16

Mfumu Herode anafuna kupha Yesu. Sanafune Yesu kukhala Mbuye. Koma Mulungu anasamalira Yesu ndipo Yesu sanaphedwe. Munthu aliyense yemwe akana Yesu kukhala Mbuye wa moyo wake adzakhala ku Gehena kopanda Mulungu.

# Yesu anaitana anthu kumulondola

Ine ndidzakutsatani kumene kuli konse mukapitako – Luka 9.57b

**26 August – Yohane Mbatizi**

<u>Werengani Mateyu 3.1-4 ndi 3.13-17</u>

Yohane, mwana wa mwamuna wa Zakariya ndi Elizabeti, anakula. Analalikira kuti anthu ayenera kulapa macimo ao. Anatinso kuti Yesu adzabwera posacedwa. Anthu ena anaulula macimo ao nalapa. Anabatizidwa ndi Yohane. Cifukwa ca ici Yohane achedwa Yohane Mbatizi. Ubatizo usonyeza za kusambitsidwa ku macimo ndi Yesu. Yesu anafunanso kubatizidwa. Koma analibe chimo. Yohane anakana kumubatizira. Yohane atauzidwa ndi Yesu kuti Mulungu afuna Iye kukhala wobatizika, anabvomera. Atabadwa Yesu Mulungu anati kuti Yesu ndiye Mwana wake.

**Funso: Kodi kulondola Yesu kutanthauza ciani kwa inu?**



**27 August – Ophunzira oyamba a Yesu**

Werengani Yohane 1.35-42

Yohane Mbatizi anacha Yesu *Mwanawankhosa wa Mulungu.* Yesu anafa pa mtanda monga nkhosa zinaperekedwa nsembe kwa Mulungu. Yohane ndi Andreya anamva mau a Yohane. Analondola Yesu. Simoni, m'bale wake wa Andreya, anamulondolanso.

**28 August – Ophunzira ena**

Werengani Yohane 1.43-51

Filipo, Natanayeli ndi anthu ena analondola Yesu cifukwa anaitanidwa naye. Anakhulupirira kuti Yesu ndiye Mwana wa Mulungu. Yesu atiitananso kumutsata. Tilondola Ambuye Yesu pamene timumvera.

**29 August – Levi anaitanidwa**

Werengani Luka 5.27-32

Ayuda (ndiwo Aisrayeli) anakhoma msonkho kwa Aroma amene anawalamulira. Levi anali wamsonkho. Nthawi zambiri amsonkho ndiwo akuba. Yesu anaitana Levi kumutsata. Levi (kapena Mateyu) anakhala mmodzi wa ophunzira 12 a Yesu.

**30 August – Ana ang'ono**

Werengani Marko 10.13-16

Nthawi zina anthu aganiza kuti ana si ndiwo ofunikira. Kwa Yesu ndiwo ofunikira kwambiri. Afuna ana kukhala pafupi naye. Kulibe mwana mmodzi yemwe ali wocepa kwambiri kuti asatsate Yesu.

**31 August – Zakeyu**

Werengani Luka 19.1-6

Zakeyu anali wakuba. Anafuna kuona Yesu. Yesu anadziwa zimene zinali m'mtima wake. Anaitana Zakeyu. Yesu ndiye wacifundo.

**1 September – Anthu otayika**

Werengani Luka 19.7-10

Anthu sanakondwere poona Yesu kupita ku nyumba ya Zakeyu. Yesu anati kuti anadza kupulumutsa anthu otayika. Afuna kuti anthu ocimwa amva cisoni pa macimo ao nakuwaleka ndiponso kuti amulondola. Kodi mukumva monga wotayika?

# Zodabwitsa zimene Yesu anacita

Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi – Mateyu 28.18b

**2 September – Munthu wamanjenje anaciritsidwa**

Werengani Luka 5.17-26

Pamene Ambuye Yesu anali pa dziko lapansi anacita zodabwitsa zambiri. Zodabwitsa zinasonyeza kuti Yesu ndiye Mwana wa Mulungu ndithu.

Lero tawerenga za codabwitsa cimodzi. Anzake anai anabweretsa mwamuna wodwala kwa Yesu. Anzake awa anali anzake abwino. Anadziwa kuti ndi Yesu yekha amene akwaniritsa kuwathandiza. Anacotsa tsindwi ya nyumba cifukwa anafuna mnzao wodwala kukhala pafupi ndi Yesu. Yesu anakhululukira macimo a mwamuna. Anamuciritsanso. Yesu ndi wamphamvu woposa uchimo ndi matenda.

**Funso: Ndi cifukwa ciani ndi Yesu yekha amene akwaniritsa kukuthandizani m'mabvuto?**



**3 September – Wakhate anaciritsidwa**

Werengani Marko 1.40-45

Akhate sanaloledwe kubwera pafupi ndi anthu ena cifukwa ca nthenda yao. Cimodzi-modzi anthu ocimwa saloledwa kukhala pafupi ndi Mulungu cifukwa ca uchimo wao. Yesu anaciritsa wakhate. Yesu Kristu akwaniritsa kukuciritsani ku uchimo wanu.

**4 September – Namondwe**

Werengani Marko 4.35-41

Kulibe munthu amene angalamulire cilengedwe. Koma Ambuye Yesu akhoza. Akwaniritsa kucita kalikonse komwe afuna. Yesu ndiye Mulungu.

**5 September – Legio**

Werengani Marko 5.1-13

Legio analamuliridwa ndi Satana. Satana analamulira umoyo wake. Mulungu anaonetsa kuti Iye ndiye wamphamvu woposa Satana. Akhoza kugonjetsanso Satana ndi uchimo m'umoyo wanu.

**6 September – Mwana wakufa anaukitsidwa**

Werengani Marko 5.21-24 ndi 5.35-43

Yesu ndi wamphamvu woposa imfa. Iye ndiye Mwana wa Mulungu. Baibulo likamba kuti anthu onse ndiwo akufa m'uzimu kaamba ka uchimo. Olandira umoyo wa m'uzimu ndiwo amoyo m'uzimu. Kodi mwalandira umoyo wa m'mzimu wocokera kwa Mulungu?

**7 September – Cakudya cinaculuka**

Werengani Marko 6.35-44

Yesu anasamalira anthu okhala ndi njala. Anadziwa zimene iwo afunika. Anawapatsa zimene afunika. Yesu atisamaliranso m'miyoyo yathu ya masiku onse. Akwaniritsa kutithandiza pa ciriconse comwe tifunika.


**8 September – Bartimeyo wakhungu**

Werengani Marko 10.46-52

Yesu anaciritsa Bartimeyo. Baibulo likamba kuti anthu ocimwa ndiwo monga akhungu. Yesu yekha akhoza kutipatsa maso a uzimu kuti timvetsetsa ndi kukhulupirira Baibulo.

# Cikhulupiriro

Ndipo lamulo lace ndi ili, kuti tikhulupirire dzina la Mwana wace Yesu Kristu – 1 Yohane 3.23a



**9 September – Kukhulupirira m'Yesu**

Werengani Yohane 20.30 ndi 31

Masabata atha tinaphunzira zambiri za Ambuye Yesu. Yesu anacita zodabwitsa zambiri. M'ndime zimene tawerenga lero tawerenga colinga ca zodabwitsa zimene Yesu anacita. Yesu anafuna kuphunzitsa anthu. Anafuna kuti akhulupirire kuti Iye ndiye Mwana wa Mulungu. Ndiye cikhulupiriro ciri pa Mulungu ndipo makamaka pa Yesu.

Mzimu Woyera apatsa cikhulupiriro ici coona m'mtima. Anthu amene akhala ndi cikhulupiriro coona adalira pa Mulungu pa cipulumutso cake. Adzipereka kwa Iye. Mwa cisomo alandira cikhululukiro ca macimo mwa Yesu.

**Funso: Kodi ndinu wokopedwa m'mtima wanu kuti macimo anu akhululukidwa ndi Yesu?**

**10 September – Kulapa**

Werengani Marko 1.14 ndi 15

Tiyenera kumva cisoni pa macimo athu ndiponso kutsutsana nao. Munthu aliyense wokhululukidwa ndi Yesu akuda uchimo.

**11 September – Cikhulupiriro ndi cofunika**

Werengani Yohane 3.14-20

Macimo athu akhululukidwa cabe ngati tikhulupirira Yesu mwa cikhulupiriro coona. Mukakhulupirira Yesu mukhala ndi moyo wosatha. Ngati simukhulupirira Yesu mulibe moyo wosatha. Kodi mukhala ndi cikhulupiriro coona copulumutsa?

**12 September – Mphatso yocokera kwa Mulungu**

Werengani Aefeso 2.8 ndi 9

Anthu onse aperewera kulapa ndi kukhulupirira Yesu moonadi. Mulungu Mzimu Woyera apangitsa anthu kukhala olapadi ndi okhulupiriradi. Mupempheni kulapa ndi cikhulupiriro. Mulungu afuna kukupatsani izi.

**13 September – Yesu yekha**

Werengani Agalatia 2.16

Kulibe munthu amene angapulumuke ku macimo ake mwa zocita zake. Tikafuna kupulumutsidwa sitiyenera kupatsa kalikonse kwa Mulungu. Yesu yekha apulumutsa ku uchimo. Kupulumutsa ndiko nchito yake.

**14 September – Cikhulupiriro ndi nchito**

Werengani Yakobo 2.14-20

Nchito zathu sizitipulumutsa. Zocita zathu zionetsa ngati cikhulupiriro cathu ndi coona. Miyoyo yathu ya masiku onse ionetsa ngati Yesu ndi wofunikira kwa ife. Kodi moyo wanu wa masiku onse uonetsa ciani?

**15 September – Khulupiriirani lero**

Werengani Luka 13.6-9

Mtengo m’nthano sunabale zipatso. Mwini wake anali wodekha. Mulungu ndi wodekha kwa ife. Atipatsa nthawi kuti tilape ndi kukhulupirira Yesu. Tikafa tidzacedwa kwambiri. Lapani lero. Khulupiririrani Yesu lero.

# Yesu aphunzitsa m'nthano

Iye wakukhala ndi Mwana ali nao moyo; wosakhala ndi Mwana wa Mulungu alibe moyo – 1 Yohane 5.12



**16 September – M'busa ndi nkhosa zake**

<u>Werengani Luka 15.3-7</u>

Yesu anauza nthano zambiri. Nthano izo zichedwa mafanizo. Yesu anazigwiritsa nchito kuti aphunzitse anthu. M'nthano iriyonse imene Yesu anauza muli phunziro.

Lero tawerenga fanizo limodzi. M'busa anali ndi nkhosa 100. Anazisamalira. Anazipatsa zofunika zao zonse. Tsiku lina nkhosa imodzi inasowa. Anamva cisoni cacikulu. Anapita kukapeza nkhosa yotayika. Ataipeza anaisenza. Anaibweretsanso kunyumba. Anthu onse anakondwera.

Yesu ndiye M'busa Wabwino. Anthu ocimwa ndiwo monga nkhosa iyo yotayika. Kopanda Yesu ndife otayika. Yesu afunafuna anthu otayika, monga m'busa anafunafuna nkhosa yotayika. Kumwamba kuli cimwemwe pamene nkhosa yotayika yapezedwa. Mukalapa ku macimo anu kuli cimwemwe Kumwamba. Mulungu afuna anthu kubweranso kwa Iye.

**Funso: Kodi kutanthauza ciani kwa inu kuti Yesu ndiye M'busa Wabwino?**

**17 September – Kondani anthu onse**

Werengani Luka 10.25-37

Wansembe ndi Mlevi anali anthu opembedza. Sanathandize munthu wobvutika. Asamariya anali adani a Ayuda. Koma Msamariya anasamalira wodwalayo. Mulungu afuna kuti tizikonda ndi kuthandiza munthu wina aliyense.

**18 September – Kucoka ku nyumba ya tate**

Werengani Luka 15.11-16

Mwana wa mwamuna wamng'ono anasiya nyumba ya tate wake. Cifukwa ca uchimo ndiri monga mwana wa mwamunayo. Ndiri kutali ndi Mulungu. Kopanda Mulungu ndife m'cipsinjo.

**19 September – Kubweranso kunyumba**

Werengani Luka 15.17-24

Patapita nthawi mwana wa mwamuna anazindikira kuti anayenera kupita kunyumba. Tate wake anakondwera. Mulungu afuna kuti tilape ndi kubweranso kwa Iye.

**20 September – Wolemera kapena wosauka?**

Werengani Luka 12.16-21

Mwamuna m'fanizo anali ndi zinthu zambiri koma sanali mwana wa Mulungu. Anali wosauka ndithu. Mukakhala kopanda ndalama zambiri koma ndinu mwana wa Mulungu ndinu wolemera. Nanga inu? Ndinu wolemera kapena wosauka?

**21 September – Kuitanidwa ku ukwati**

Werengani Mateyu 22.1-10

Anthu anaitanidwa kubwera ku ukwati. Ambiri anakana. Ife taitanidwa kubweranso kwa Mulungu. Kodi mwakana kulapa?

**22 September – Kusowa zobvala za ukwati**

Werengani Mateyu 22.11-14

Kunali munthu amene anasowa zobvala zokhoza za ukwati. Sanakonzeke. Tiyenera kukhala okonzeka kupita Kumwamba. Tingalowe cabe ngati tiri ndi mtima watsopano (umoyo wa uzimu).

# Maphunziro ena amene Yesu aphunzitsa

Wokonda mwambo akonda kudziwa; Koma wakuda cidzudzulo apulukira – Miyambi 12.1



**23 September – Nyumba ziwiri**

Werengani Mateyu 7.24-27

Mwamuna anamanga nyumba. Poyamba anakumba mpaka anapeza maziko abwino. Kucita tero kunali nchito yaikulu. Mwamuna wina anamanganso nyumba. Anamanga mofulumira. Anatsiriza msanga.

Mvula inalokwa. Mphepo inaomba. Nyumba yomangidwa msanga inagwa. Nyumba yomangidwa pa tanthwe siinagwe.

Maziko abwino ndi ofunikira kwambiri. Ngati Yesu ndiye maziko athu ndife otetezeka. Tiyenera kumumvera. Ngati sitimamvera Iye ndife monga munthuyo wopusa.

**Funso: Kodi ndinu wanzeru kapena wopusa pa maso pa Mulungu?**

**24 September – Ndalama yopezedwa**

Werengani Luka 15.8-10

Mkazi m'nthano anataya ndalama. Tikataya ndalama tiisakira. Tikondwera takaipeza. Baibulo litiuza kuti angelo akondwera pamene wocimwa wotayika apezedwa.

**25 September – Cotupitsira mkate**

Werengani Mateyu 13.33

Tikapanga mkate tifunika cotupitsira. Cotupitsira cimasintha ufa. Yesu anauza kuti Ufumu wa Mulungu uli monga cotupitsira mkate. Ufumu wa Mulungu ndiwo anthu a Mulungu. Yesu ndiye Mfumu wao. Ufumu wa Mulungu suoneka kome uli ndi mphamvu.

**26 September – Ufumu wa Mulungu umakula**

Werengani Mateyu 13.31 ndi 32

Pa nthawi yake ya pa dziko lapansi Ufumu wa Yesu unaoneka waung'ono. Anthu omukhulupirira anali ocepa. Koma pambuyo pake ambiri adzamu-khulupirira. Yesu anati kuti Ufumu wake uli monga mbeu. Mbeu yaing'ono ikhala mtengo waukuludi.

**27 September – Cuma**

Werengani Mateyu 13.44-46

Nthawi zambiri anthu afunafuna cuma. Yesu Kristu ndiye cuma cacikulu coposa. Ngati muli ndi Yesu ndinu wolemera. Kodi mumacita ciani kuti mupeze Yesu?

**28 September – Kufuna kuthandiza**

Werengani Luka 11.5-13

Mwamuna wobvutika anapita kwa mnzake kukapeza thandizo. Mnzake sanafune kuthandiza. Mulungu amafuna kutithandiza nthawi zonse. atipatsa Mzimu Woyera ngati timupempha.

**29 September – Kupempherabe**

Werengani Luka 18.1-8

Mkazi wobvutika anapita kwa woweruza kukapempha thandizo. Woweruza sanafune kumuthandiza. Mkazi anapitirizabe kupempha. Potsiriza woweruza anathandiza. Mulungu afuna kuti timapempherabe, angakhale sayankha msanga.

# Anthu omwe Yesu anakomana nao

Yehova ndiye wabwino ndi wolunjika mtima: Cifukwa cace adzaphunzitsa olowa za njira – Salimo 25.8

**30 September – Nikodemo**

<u>Werengani Yohane 3.1-8</u>

Nikodemo anali Mfarisi. Afarisi anaganiza kuti apulumuke posunga malamulo a Mulungu. Yesu anauza Nikodemo kuti ayenera kubadwa mwatsopano asanakhale m'Ufumu wa Mulungu. Anthu onse ayenera kubadwa mwatsopano.

Tinaphunzira kale kuti Adamu ndi Hava anacimwa. Kucokera ku nthawi iyo munthu aliyense ndiye wocimwa. Sitikwaniritsa kusacimwa, cifukwa mitima yathu ndi yocimwa. Ganizirani za citsanzo ca citsime. Ngati madzi apansi pa citsime sali bwino, madzi onse m'citsime sali bwino. Ngati mitima yathu ndi yocimwa, umoyo wathu wonse ndi wa uchimo. Masiku onse tilephera kukonda Mulungu kuposa anthu onse ndi kukonda anansi.

Yankho lenileni ndilo kulandira mtima watsopano wocokera kwa Mulungu. Ici citanthauza kulandira umoyo wa uzimu. Mulungu Mzimu Woyera amasintha mitima ndi miyoyo. Ici cichedwa kubadwa mwatsopano. Pamene Mzimu Woyera afuna kupatsa munthu umoyo wa uzimu, cicitika. Munthu wobadwa mwatsopano amva cisoni pa mtima wake wocimwa, alapa ndi kukhulupirira Yesu pa cipulumutso cake. Afuna kumvera Mulungu nthawi zonse.

**Funso: Kodi ndinu wobadwa mwatsopano?**



**1 October – Mkazi wa ku Samariya**

Werengani Yohane 4.4-15

Ayuda ndi Asamariya anali adani. Yesu anapempha madzi kwa mkazi wa ku Samariya. Pamene Yesu analankhula za madzi amoyo anatanthauza Mzimu Woyera. Mzimu Woyera apatsa umoyo wa uzimu.

**2 October – Kuphunzitsa mkazi**

Werengani Yohane 4.16-30

Yesu adziwa zonse. Adziwa macimo omwe tinacita. Anauza mkazi kuti Iye ndiye Mpulumutsi. Mkazi anauza anthu ena za Yesu. Anafuna kuti iwonso adziwe Yesu.

**3 October – Asamariya**

Werengani Yohane 4.39-42

Asamariya ambiri anapita kwa Yesu. Yesu anawaphunzitsa za Iye yemwe. Asamariya analapa namukhulupirira. Analandira madzi amoyo. Analandira umoyo wa uzimu. Kodi mwalandira umoyo wa uzimu?

**4 October – Mkazi wocimwa**

Werengani Luka 7.36-50

Yesu anafotokoza kuti anthu okhululukidwa ku macimo ambiri akonda Yesu kuposa iwo amene sanacite macimo ambiri. Tizipempha Ambuye Yesu cikhululukiro. Mungakhale munacita macimo ambiri.

**5 October – Munthu wolemera**

Werengani Mateyu 19.16-22

Mwamuna anasunga malamulo a Mulungu. Yesu anamuuza kuti agulitse zonse zimene zinali nazo. Mwamuna anakana kucita tero. Anakonda katundu wake kuposa Mulungu. Zocita zake zinali zabwino, koma mtima wake sunali wabwino.

**6 October – Marita ndi Mariya**

Werengani Luka 10.38-42

Marita anasamalira alendo. M’bale wake sanamuthandize, koma iye anamvera Yesu Mphunzitsi. Yesu anauza Marita kuti sayenera kuiwala cofunikira coposa: ndico Yesu ndi cipulumutso cake. Ndi ciani cimene ciri cofunikira coposa m’umoyo wanu?

# Yesu anagwiridwa

## Amene anaperekedwa cifukwa ca zolakwa zathu – Aroma 4.25a

**7 October – Ciwembu**

Werengani Luka 22.3-6

Yesu ankacita zabwino cabe. Anaphunzitsa anthu za Mulungu. Anathandiza obvutika.

Anthu ambiri anatsata Yesu nakhala okondwera. Ena sanakondwere, makamaka atsogoleri a cipembedzo (Afarisi ndi Asaduki). Sanafune kumvera Yesu. Anaganiza kuti safunika Yesu. Anaganiza kuti adzaloledwa Kumwamba cifukwa ndiwo acipembedzo kwambiri. Sanafunika Yesu kufika Kumwamba. Anada Yesu. Anafuna kumupha. Yudase anali mmodzi wa ophunzira 12 a Yesu. Anali wopereka kwa adani. Anafuna kuthandiza Afarisi ndi Asaduki kuti aphe Yesu. Anabvomerezana kuti Yudase adzalipiridwa pocita tero.

**Funso: Kodi mufunika Yesu kuti akupulumutseni ku macimo anu? Kapena mufuna kudzipulumutsa?**



**8 October – Cisangalalo**

Werengani Luka 22.7-13

Cikondwerero ca Pasaka cinakumbutsa Ayuda za kupulumutsidwa kwa Aigupto zaka zakale. Yesu anafuna kukondwerera ndi ophunzira ake. Yesu anatuma Petro ndi Yohane kukonzekera cisangalalo.

**9 October – Yesu anadzicepetsa**

Werengani Yohane 13.3-17

Aisrayeli ankasamba mapazi ao asanadye. Nthawi zambiri wanchito kapena kapolo ndiye anali kucita. Lero tawerenga kuti Yesu anasamba mapazi. Yesu anadzicepetsa. Afuna kuti tidzicepetsanso.

**10 October – Yesu adzagwiridwa**

Werengani Luka 22.14-21 ndi 22.31-34

Yesu anauza ophunzira ake kuti adzafa ndi kukhalanso ndi moyo. Petro sanafune Yesu kufa. Yesu anati kuti Petro adzamukana m'malo mwa kumuthandiza. Yesu anayenera kufera Petro kuti iye apulumuke.

**11 October – M'munda wa Getsemane**

Werengani Mateyu 26.36-46

Yesu anabvutika. Ophunzira ake sanamuthandize koma anagona. Yesu anapemphera kuti kufuna kwa Mulungu kucitike. Mulungu anafuna Yesu kuzunzika nafa. Cifukwa ca Yesu ana ake ali ndi mtendere, citonthozo ndi umoyo wosatha.

**12 October – Yesu anaperekedwa ndi Yuda**

Werengani Yohane 18.1-9

Yuda ndi anthu ena anadza kugwira Yesu. Yesu anawaonetsa kuti Iye ndiye wamphamvu zonse. Anthu anakwaniritsa kumugwira cabe cifukwa Iye anawalola kucita tero. Yesu anadzipereka kugwiridwa. Anafuna kukhala Mpulumutsi.


**13 October – Yesu anayenera kufa**

Werengani Mateyu 26.51-56

Yesu anafotokoza cifukwa cake anayenera kufa. Yesu anayenera kucita zimene Mulungu anafuna kuti acite. Yesu anafuna kucita cifuniro ca Mulungu. Nanga inu, mufuna kucita kufuna kwa Mulungu?

# Yesu anafa pa mtanda

Ndipo palibe cipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina pansi pa thambo la kumwamba lopatsidwa mwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo – Macitidwe a Atumwi 4.12



**14 October – Yesu anafunsidwa ndi Kayafa**

Werengani Mateyu 26.57-68

Yesu anaperekedwa kwa Kayafa. Kayafa anali mkulu wa ansembe, mtsogoleri wa anthu a cipembedzo. Iye ndi anthu ena ofunikira anafunsa Yesu mafunso. Anafunafuna kupeza colakwa ca Yesu. Sanacipeze. Yesu sanalakwe kalikonse.

Kenaka anthu ananena mabodza a Yesu. Kunena bodza ndiko chimo. Yesu sanawayankhe.

Pamene Kayafa anafunsa Yesu ngati Iye ndiye Mwana wa Mulungu Yesu anamuyankha. Anati kuti ndiye Mwana wa Mulungu. Mkulu wa ansembe anakalipa. Ananena kuti Yesu ananyenga Mulungu. Iwo anafuna Yesu kuphedwa.

**Funso: Kodi mukumva bwanji za imfa ya Yesu?**

**15 October – Petro**

<u>Werengani Mateyu 26.69-75</u>

Petro anati kuti sadziwa Yesu. Anakana Yesu. Petro anazindikira kuti adacimwa. Anamva cisoni kwambiri nalira. Kodi mumamva bwanji mutacimwa?

**16 October – Pa maso pa Pilato**

<u>Werengani Mateyu 27.11-25</u>

Pilato anayenera kuweruza Yesu. Anadziwa kuti Yesu sanalakwe. Analola anthu kusankha kumasula Baraba (wakupha) kapena Yesu. Anthu anafuna Yesu kufa. Ndiwo oipa. Anthu ocimwa ndiwo oipa.

**17 October – Yesu anazunzidwa**

<u>Werengani Mateyu 27.26-31</u>

Anthu anabvutitsa kwambiri Yesu. Anazunza Yesu. Anamunyoza. Anamupereka ku malo opacikidwirako kuit ampacike.

**18 October – Ocita zoipa**

<u>Werengani Luka 23.32-43</u>

Pamene Yesu anabvutika anapempherera adani ake. Tiyeneranso kupempherera adani athu. Anthu ocita zoipa anapacikidwa pafupi naye. Mmodzi wa iwo anapemphera cifundo ca Mulungu. Anacilandira.

**19 October – Yesu anafa**

<u>Werengani Mateyu 27.45-50</u>

Pa nthawi ya 12 koloko kunada. Mulungu anasiya Yesu. Kusiyidwa ndi Mulungu ndiko cilango ca uchimo. Yesu anasenza cilango ca ana ake. Iwo sadzasiyidwa ndi Mulungu nthawi zonse. Timakumbukira imfa ya Yesu pa Lacisanu Loyera.


**20 October – Kuuikidwa m'manda kwa Yesu**

<u>Werengani Mateyu 27.57-66</u>

Yesu adafa. Anaikidwa m'manda. Ayuda anakumbukira Yesu ponena kuti adzauka kwa akufa. Anaopa. Anaika asirikali olonda manda. Kunalibe munthu wololedwa kudza pafupi ndi manda.

# Cisomo ca Mulungu

Cisomo kwa inu ndi mtendere za kwa Mulungu Atate wathu ndi Ambuye Yesu Kristu – Afilipo 1.2



**21 October – Wamsonkho**

Werengani Luka 18.9-14

Yesu anafa pa mtanda. Cifukwa ca imfa yake, anthu ake apulumuka ku macimo ao. Kupulumutsidwa ndiko mphatso mwa cisomo yocokera kwa Mulungu. M'nthano imene tawerenga m'Baibulo Yesu anafotokoza za cisomo.

Amuna awiri anapita ku Kacisi. Mmodzi anali Mfarisi. Anadziwa zambiri za Mulungu. Anasunga malamulo a Mulungu. Popemphera anayamika Mulungu. Anayamika Mulungu kuti iye si ndiye munthu woipa. Anati kuti amacita zabwino zambiri. Sanafunike kalikonse kocokera kwa Mulungu. Mwamuna wina anali wamsonkho. Wamsonkho anamva manyazi. Anadziwa kuti anacita zoipa. Anamva cisoni pa kucimwa kwake. Popemphera anapempha cifundo ca Mulungu cabe.

M'Baibulo tawerenga kuti Mulungu anakhululukira macimo a wamsonkho. Wamsonkho sanapatsidwe cilango cimene anayenera. Ico ndi cisomo. Ndi mphatso yaikulu yocokera kwa Mulungu wacisomo!

**Funso: Kodi cisomo ca Mulungu citanthauza ciani kwa inu?**

**22 October – Mphatso ya Mulungu**

Werengani Aefeso 2.1-10

Anthu onse acimwa. Mtima wa aliyense ndi wocimwa monga mtima wa alionse. Cikhululukiro ca macimo ndico mphatso ya Mulungu. Umoyo wa uzimu ndi mphatso ya Mulungu. Cisomo ndi cikondi ca Mulungu ndi zazikulu. Tiribe cifukwa cake ca kudzikweza.

**23 October – Yesu**

Werengani 2 Timoteo 1.8-10

Tikacimwa tilakwira Mulungu. Sitikwaniritsa kucita kalikonse kumukondweretsa. Koma Yesu akwaniritsa. Anafa kukululukira macimo. Mulungu anakondwera pa ico. Tilandire cisomo cifukwa ca Yesu Kristu.

**24 October – Lapani**

Werengani Yoweli 2.13 ndi 14

Tiyenera kutha psiti cifukwa ca macimo athu. Baibulo litiuza kulapa. Mulungu ndiye wacifundo. Mupempheni cikhululukiro mwa cisomo. Kaciteni ndi mtima wanu wonse.

**25 October – Cifundo ca pa masiku onse**

Werengani Maliro 3.21-24

Nthawi zambiri tiri ndi mabvuto m'miyoyo yathu. Tikapenyetsetsa macimo athu tiyenera kukomana ndi mabvuto ena ambiri. Kungakhale tiri m'macimo, Mulungu ndiye wacifundo masiku onse.

**26 October – Khalani wacifundo**

Werengani Mateyu 18.23-35

Masiku onse Mulungu amaticitira cifundo. Tiyenera kucitiranso cifundo anthu ena. Makamaka ngati mudziwa kuti Mulungu anakukhululukirani macimo anu mwa cisomo. Muzikhululukiranso anthu ena amene akucitirani coipa.

**27 October – Khalani umoyo wanu kwa Mulungu**

Werengani Tito 2.11-14

Ngati mudziwa kuti munalandira cisomo ca Mulungu, muyenera kukhala umoyo wanu kwa Mulungu. Muzimvera. Muyenera kuganizira mphatso yaikulu imene Mulungu anakupatsani.

# Yesu anauka kwa akufa

Yesu anati kwa iye, Ine ndine kuuka ndi moyo; wokhulupirira Ine, angakhale amwalira, adzakhala ndi moyo – Yohane 11.25

**28 October – Yesu anauka**

<u>Werengani Mateyu 28.1-9</u>

Pambuyo pa kuuikidwa m'manda kwa Yesu, akazi anapita ku manda kwake. Asanafikeko kunali cibvomezi. Mngelo anatsika Kumwamba. Anaoneka monga mphezi. Zobvala zake zinali zoyera. Asirikali anaopa. Anathawa. Mngelo anatsegula manda.

Akazi anaopa poona manda wotsegulidwa. Mngelo anawauza kuti asaope. Anayenera kukondwera. Yesu anauka kwa akufa. Anacoka m'manda.

Yesu akhala ndi moyo! Cifukwa cake akwaniritsa kutipatsa umoyo wa uzimu. Caka ciriconse timakumbukira kuuka kwake pa tsiku la Pasaka.

**Funso: Kodi kuuka kwa Yesu kutanthauza ciani kwa inu?**



## 29 October – Ku manda

Werengani Yohane 20.3-10

Awiri a ophunzira a Yesu anamva kuti Yesu adauka. Anapita ku manda. Anapeza nsalu zabafuta cabe. Ico cinatsimikizira kuti Yesu anauka ndithu.

## 30 October – Mariya wa Magadala

Werengani Yohane 20.11-18

Mariya wa Magadala anasowa Yesu. Yesu anadzibvumbulutsa kwa iye. Anati kuti adzapita kwa Atate ake Kumwamba. Mariya anayenera kuuza ophunzira ena uthenga wabwino. Kodi mumafalitsa uthenga wabwino wa kuuka kwa Yesu?

## 31 October – Amuna awiri

Werengani Luka 24.13-27

Amuna awiri anadera nkhawa. Adamva kuti Yesu adauka, koma sanamvetse. Yesu anakomana nao. Iwo sanamudziwe. Yesu anafotokoza kuti adayenera kufa ndi kuuka kwa akufa.

## 1 November – Yesu anadzibvumbulutsa

Werengani Luka 24.28-35

Amunawo awiri anapempha Yesu kukhala nao. Yesu anadzibvumbulutsa kwa iwo. Kodi mumapempha Yesu kukhala nanu?

## 2 November – Yesu anayendera ophunzira ake

Werengani Yohane 20.19-25

Ophunzira anabvala zitseko. Kunalibe munthu amene angalowe. Mwadzidzidzi Yesu analowa. Anawaonetsa manja ndi mapazi ake. Iwo anaona zizindikiro za misomali ya mtanda. Iye anali Yesu ndithu. Anakondwera kwambiri.

## 3 November – Tomasi

Werengani Yohane 20.26-31

Tomasi kunalibe pa nthawi yoyamba pamene Yesu anadzibvumbulutsa kwa ophunzira ake. Patapita sabata limodzi Yesu anadzibvumbulutsa kwa Tomasi. Tomasi anaulula kuti Yesu ndiye Mbuye ndi Mulungu wake. Kodi Yesu ndiyenso Mbuye ndi Mulungu wanu?

# Yesu anakwera Kumwamba natuma Mzimu Woyera wake

Bukutsani mwa mitundu ya anthu zocita Iye – Salimo 105.1b



**4 November – Lamulo la Yesu**

Werengani Mateyu 28.18-20

Yesu anayenderanso ophunzira ake. Anawauza kuti ali ndi mphamvu zonse. Iwo sayenera kuopa. Yesu anawapatsa lamulo. Ophunzira anayenera kuuza anthu ena za Yesu. Anthu onse azimva uthenga wabwino wa Yesu. Onse ayenera kumvera Mulungu. Yesu anauza ophunzira ake kuti sayenera kudera nkhawa kapena kuopa. Yesu adzakhala nao nthawi zonse. Angakhale adzapita ku maiko ena kukauza anthu ena za Iye. Mulungu sadzasiya anthu ake.

**Funso: Kodi mwaphunzira ciani m'ndime izi?**

**5 November – Yesu anakwera kunka Kumwamba**

Werengani Macitidwe a Atumwi 1.4-9

Yesu anauza ophunzira ake kuyembekezera Mzimu Woyera. Mzimu Woyera adzawathandiza kulalikira. Yesu atatsiriza kuwalangiza anakwera Kumwamba. Caka ciriconse timakumbukira kukwera kwake pa Tsiku lokumbukira kukwera Kumwamba kwa Yesu.

**6 November – Yesu atakwera Kumwamba**

Werengani Macitidwe a Atumwi 1.10-14

Angelo awiri anauza ophunzira kuti Yesu adzabwera-nso. Ophunzira anapita ku Yerusalemu napempha Mzimu Woyera. Mzimu Woyera ndi Mulungu, monga Atate ndi Yesu. Mulungu ndiye mmodzi, koma mo-mwemo muli Atatu. Ici cichedwa Utatu wa Mulungu.

**7 November – Mzimu Woyera anadza**

Werengani Macitidwe a Atumwi 2.1-13

Mulungu anatuma Mzimu Woyera wake. Anthu onse anamva uthenga wa Mulungu m'cilankhulo cao. Anthu onse anamvetsa zimene Mulungu ananena. Caka ciriconse pa Tsiku la Pentekositi timakumbukira kuti Mzimu Woyera anatumidwa ndi Mulungu.

**8 November – Malongosoledwe a Petro**

Werengani Macitidwe a Atumwi 2.14-21

Anthu ena anaganiza kuti ophunzira analedzera. Petro anafotokoza kuti sanaledzere. Zonse zocitika zinali zizindikiro za Mzimu Woyera. Petro anaphunzitsa anthu za Yesu Kristu (Macitidwe a Atumwi 2.22-36).

**9 November – Anthu ambiri analapa nakhulupirira**

Werengani Macitidwe a Atumwi 2.37-41

Anthu ambiri anamva kuti afunika cipulumutso ca macimo ao. Analapa ndipo anabatizidwa. Anasanduka ana a Mulungu. Anachedwa Akristu pakuti anali a Yesu Kristu. Tsiku ilo linali tsiku lokondweretsa. Mphamvu ya Mulungu ndi yaikulu.

**10 November – Kulemekeza Mulungu**

Werengani Macitidwe a Atumwi 2.42-47

Iwo amene anapulumutsidwa anakondwera. Analemekeza Mulungu pa zimene anawacitira. Masiku onse Mulungu anaonjezera anthu olapa ndi okhulupirira mwa Yesu. Mzimu Woyera anagwiradi nchito.

# Yesu adzabweranso

Cifukwa cace dikirani, pakuti simudziwa tsiku lace lakufika Ambuye wanu Mateyu 24.42



**11 November – Asanabwerenso Yesu**

Werengani Mateyu 24.3-14

Tsopano Yesu ali Kumwamba. Anati kuti adzabweranso. Yesu anaphunzitsa ophunzira ake pa zimene zidzacitika asanabwerenso. Anthu adzabvutika kwambiri. Kudzakhala nkhondo, zibvomezi, matenda ndi njala. Akristu adzazunzidwa. Otsogolera a cipembedzo adzasokeretsa anthu ena. Adzakamba mabodza a Yesu. Anthu ambiri adzawakhulupirira nakhala olakwa. M'masiku ano tiyembekezera kubweranso kwa Yesu. Tiona zacisoni izo zimacitika pafupi nafe. Tikamva izi tkumbutsidwa kuti Yesu adzabweranso.

**Funso: Kodi ndinu wokonzeka kwa kubweranso kwaciwiri kwa Yesu?**

**12 November – Kuonedwa ndi anthu onse**

Werengani Mateyu 24.29-31

Pamene Yesu adzabweranso kudzakhala zodabwitsa za m'cilengedwe. Adzadza m'thambo. Anthu onse adzamuona. Angelo adzasonkhanitsa okhulupirira oona onse. Kodi mudzakondwera pamene Yesu abweranso?

**13 November – Mulungu sadzasanduka**

Werengani Mateyu 24.34-36

Zonse zidzasinthidwa pamene Yesu abweranso. Zonse zidzakonzedwanso. Mulungu yemwe ndi Mau ake sadzasintha. Mulungu ali amodzimodzi nthawi zonse.

**14 November – Dikirani**

Werengani Mateyu 24.42-44

Kulibe munthu amene adziwa nthawi ya kubweranso kwa Yesu. Cifukwa cake tizidikira. Kodi mungadikire bwanji kubweranso kwaciwiri kwa Yesu?

**15 November – Khalani okonzeka**

Werengani Mateyu 25.1-13

Yesu ananena nthano. Anamwali asanu anakonzeka za ukwati. Asanu ena sanakonzeke. Musakhale ocedwa kuti mulape ndi kulandira cikhululukiro. Ndife okonzeka kwa kubweranso kwaciwiri kwa Yesu titabadwa mwatsopano.

**16 November – Ciweruzo**

Mateyu 25.31-34 ndi Mateyu 25.41

Yesu adzaweruza onse: amoyo ndi akufa. Adzaweruza ngati munkamutumikira ndi mtima wonse monga Mkristu wobadwa mwatsopano. Ngati inde, mudzakhala naye m'Ufumu wake pa nthawi yamuyaya. Ngati iai, adzakutumani ku Gehena. Kodi mudzakhala kuti?

**17 November – Mulungu ndiye wodekha**

Werengani 2 Petro 3.9-15

Anthu ena anakayika. Yesu abweranso mocedwa. Mulungu atipatsa nthawi yolapa ndi kumukhulupirira kuti tikhale okonzeka. Tizikhala umoyo woyera. Tiyenera kumumvera.

# Ophunzira analalikira Yesu

Lalikira Mau; cita nao pa nthawi yace, popanda nthawi yace, tsutsa, dzudzula, cenjeza, ndi kuleza mtima konse ndi ciphunzitso

2 Timoteo 4.2



**18 November – Mwamuna wopunduka anaciritsidwa**

Werengani Macitidwe a Atumwi 3.1-8

Kucokera pa nthawi ya Pentekoste ophunzira anauza anthu za Yesu. M'dzina la Yesu, Yohane ndi Petro anaciritsa mwamuna wopunduka. Anagwiritsa nchito codabwitsa kuti alalikire Yesu (ndime za 12-26). Colinga ca Yohane ndi Petro ndico kuti anthu onse adziwe za Yesu Mpulumutsi.

**Funso: Kodi mungauze yani za Yesu sabata iri?**

**19 November – Sanaloledwe kulalikira**

Werengani Macitidwe a Atumwi Acts 4.1-7 ndi 15-21

Otsogolera anthu anakwiya. Sanafune kumva za mphamvu ya Yesu (ndime za 8-13). Analetsa Petro ndi Yohane kulalikira. Petro ndi Yohane anafuna kumvera Mulungu. Analalikirabe.

**20 November – Ku Samariya**

Werengani Macitidwe a Atumwi 8.9-13

Ophunzira anafika ku Samariya. Anthu a ku Samariya analondola Simoni wanyanga. Pamene anthu anamva za Yesu analapa nakumukhulupirira.

**21 November – Sanali wokhulupirira moonadi**

Werengani Macitidwe a Atumwi 8.14-25

Simoni wanyanga anafuna kugula mphamvu ya Mzimu Woyera. Pofuna ico anaonetsa kuti sadalape ndi kukhulupirira Yesu. Anali wodzikonda. Kodi mudzikonda inu nokha kapena Yesu?

**22 November – Petro m’ndende**

Werengani Macitidwe a Atumwi 12.5-12

Petro anamangidwa cifukwa analalikira Yesu Kristu. Kuzunzidwa ndi mbali ya kukhala Mkristu (Yohane 16.33). Mulungu anasamalira Petro. Mulungu atisamaliranso ngati timamumvera.

**23 November – Imfa ya Stefano**

Werengani Macitidwe a Atumwi 6.8-15 ndi 7.54-60

Stefano anali mtumiki wa Mulungu. Anthu sanakondwere. Anamunenera mabodza. Stefano anafotokoza kuti adalalikira Yesu pokhala Mpulumutsi (Macitidwe a Atumwi 7.1-53). Anthu anakalipa kotero kuti anapha Stefano.

**24 November – Akristu anazunzidwa**

Werengani Macitidwe a Atumwi 8.1-4

Akristu anayenera kuthawa cifukwa ca mazunzo. Kulikonse komwe anapitako analankhula za Yesu. Mulungu anasamalira anthu ake. Kodi mwabvutika cifukwa mufuna kumvera Mulungu yekha?

# Kusandulika kwa umoyo wa Saulo


Pakuti ndinatsimikiza mtima kuti ndisadziwe kanthu mwa inu koma Yesu Kristu, ndi Iye wopacikidwa – 1 Akorinto 2.2

**25 November – Saulo anakomana ndi Yesu**

<ins>Werengani Macitidwe a Atumwi 9.1-9</ins>

Sabata latha tinawerenga kuti Saulo anazunza Akristu. Saulo anada Yesu. Anapita ku Damasiko kukagwira olondolera Yesu. Mwadzidzidzi kunali kuunika. Saulo anagwa pansi. Anamva mau. Yesu analankhula naye. Yesu anamufunsa ndi cifukwa ciani amuzunzira. Posacedwa Saulo anazindikira kuti anacimwa. Anafunsa Yesu cimene ayenera kucita. Yesu anamuuza kupita ku Damasiko. Saulo anaimirira. Anali wakhungu. Anaperekedwa ku Damasiko.

Mtima wa Saulo unatembenukidwa ndipo moyo wake unasanduka. Mitima ndi mimoyo ya anthu onse iyenera kutembenukidwa. M'malo mwa kusamvera Mulungu tiziphunzira kumumvera. Mupempheni mphamvu yake m'umoyo wanu kuti mumumvere.



**Funso: Kodi mtima ndi umoyo wanu unatembenuka?**

**26 November – Saulo ndi Hananiya**

Werengani Macitidwe a Atumwi 9.10-20

Mulungu anatuma mtumiki wake Hananiya kwa Saulo. Hananiya anakayika. Anadziwa kuti Saulo ada Akristu. Koma Mulungu anati kuti Saulo ndiyenso mtumiki wake. Kucokera pa nthawi iyo, Saulo adzatumikira Mulungu. Patapita nthawi Saulo acedwa Paulo.

**27 November – Paulo anatumidwa kulalikira**

Werengani Macitidwe a Atumwi 13.1-3

Paulo ndi Barnaba anatumidwa ku maiko ena. Anayenera kulalikira ku anthu onse za Yesu. Asanacokeko Akristu onse anapemphera pamodzi. Kodi mumapempherera anthu olalikira?

**28 November – Mulungu yekha**

Werengani Macitidwe a Atumwi 14.8-19

Anthu a ku Lustra anafuna kulemekeza Paulo ndi Barnaba. Anati kuti ndiwo milungu. Paulo sanafune kulemekezedwa. Anafuna kuti Mulungu yekha alemekezedwe. Kodi mufuna yani kuti akalemekezedwe?

**29 November – Paulo anakomana ndi Lidiya**

Werengani Macitidwe a Atumwi 16.13-15

Paulo anakomana ndi akazi ena amene anapemphera. Analankhula nao. Lidiya anali m’modzi wa iwo. Lidiya anakhulupirira mau a Paulo. Mulungu anamupangitsa kukhala wokhulupirira. Lidiya anakonda Mulungu ndi anthu ake. Anafuna kuwasamalira.

**30 November – M’ndende**

Werengani Macitidwe a Atumwi 16.16-25

Paulo analamulira mzimu kuti uturuke m’namwali. Ambuye ake anakalipa posowa ndalama zolandiridwa. Ananenera Paulo ndi Sila mabodza. Paulo ndi Sila anaikidwa m’ndende. Anapitirizabe kulemekeza Mulungu.


**1 December – Paulo analalikirabe**

Werengani Macitidwe a Atumwi 16.26-34

Mdindo anadziwa kuti adacita zoipa. Kudzipha si yankho. Yankho lenileni la uchimo ndilo kukhulupirira Yesu. Mdindo anasamalira Paulo ndi Sila. Kodi mukonda ndi kusamalira anthu a Mulungu?

# Ulendo wa Paulo

## Pakuti Uthenga Wabwino sundicicititsa manyazi – Aroma 1.16a



**2 December – Ku Tesalonika**

<u>Werengani Macitidwe a Atumwi 17.1-9</u>

Paulo anapita ku Tesalonika. Anafotokozera Mau a Mulungu. Uthenga wake unali wa Yesu. Yesu Kristu ndiye pakatikati pa uthenga wa Mulungu. Indedi, Baibulo likambanso zambiri za mfundo zina, koma pakatikati ndi Yesu. Yesu ndiye maziko a cikhulupiriro cathu. M'ulaliki uliwonse mlaliki ayenera kuuza za Yesu amene anafa ndi kuuka kupulumutsa ocimwa. Anthu ena anakhulupirira mau a Paulo. Ena anakwiya.

**Funso: Ndi ciani cimene ciri cofunikira colalikidwa kulingana ndi inu?**

**3 December – Ku Bereya**

Werengani Macitidwe a Atumwi 17.10-13

Anthu a ku Bereya anamva uthenga wa Paulo. Anawerenga Baibulo podziwa ngati Paulo analankhula coonadi. Kodi mumawerenga Baibulo pofuna kudziwa ngati alaliki alalikira coonadi?

**4 December – Ku Korinto**

Werengani Macitidwe a Atumwi 18.1-6

Paulo analalikira ku Korinto. Ayuda sanafune kumva za Yesu. Paulo anati kuti adzaleka kuwalalikira uthenga wa Yesu. Adzapita kwa anthu ena amene sanali Ayuda. Iwo anachedwa amitundu.

**5 December – Lonjezo la Mulungu**

Werengani Macitidwe a Atumwi 18.7-11

Anthu ambiri anakana kulapa nakhulupirira Yesu. Mulungu anauza Paulo kuti asataye ciyembekezo. Angoyenera kulalikirabe. Mulungu anasamalira Paulo. Mulungu adzapanga anthu ambiri kukhala olapa ndi okhulupirira.

**6 December – Ku Efeso**

Werengani Macitidwe a Atumwi 19.13-20

Ana a mwamuna a Skeva sanali atumiki oona a Mulungu. Aefeso ambiri analapa nakhulupirira Yesu. Anatentha zoipa zao zonse za satana. Kodi muli ndi cinthu cimene Mulungu akuda? Citayeni!

**7 December – Ku Trowa**

Werengani Macitidwe a Atumwi 20.7-12

Anthu a ku Trowa anakonda kumva uthenga wa Mulungu. Mnyamata wokhala pa zenera anagwidwa ndi tulo. Anagwa pansi nafa. Paulo anamuukitsa kwa akufa. Mitima ya anthu inatonthozedwa ngakhale Paulo anayenera kuwasiya.

**8 December – Ku Kaisareya**

Werengani Macitidwe a Atumwi 21.8-14

Agabo anadza kuona Paulo. Anapereka uthenga wa Mulungu: Paulo adzagwidwa. Anthu sanafune kuti Paulo apitirize ulendo wake. Paulo anati kuti ayenera kumvera Mulungu nthawi zonse. Kodi mufuna kuti kufuna kwa Mulungu kucitike?

# Zaka zotsiriza za umoyo wa Paulo

Kuti kwapatsidwa kwa inu kwaufulu cifukwa ca Kristu, si kukhulupirira kwa Iye kokha, komatunso kumvwa zowawa cifukwa ca Iye – Afilipi 1.29



**9 December – Paulo m'mabvuto ku Yerusalemu**

Werengani Macitidwe a Atumwi 21.27-40

Paulo akalalikirabe umoyo wake udzakhala pa cipsezo. Koma Paulo sanakhoze kuleka. Anakonda Mulungu kwambiri. Anafuna kuti anthu onse amve za Yesu.

Paulo anabweranso ku Yerusalemu. Analalikira m'Kacisi. Ayuda ena anakalipa poona Paulo. Anaganiza kuti Paulo ananena zoipa za malamulo a Mulungu ndi Kacisi. Anaganiza kuti Paulo adabweretsa Ahelena m'Kacisi ndipo Ahelena sanaloledwe kulowamo. Ayuda anafuna kupha Paulo. Kapitao wamkulu anamva zonse. Anati kuti Paulo aperekedwe ku linga kumene asirikali anakhalako. Kunali mphekesera yaikulu.

M'Macitidwe a Atumwi 22 tiwerenga kuti Paulo anafotokoza kwa kapitao wamkulu zonse zimene zinacitika. Anangolalikira kuti Yesu ndiye Mpulumutsi wolonjezedwa ndi Mulungu.

**Funso: Kodi mumayankha bwanji ulaliki wa Yesu?**

**10 December – Ku Roma**

Werengani Macitidwe a Atumwi 27.14-20

Zambiri zidacitika (Macitidwe a Atumwi 22-26). Paulo anayenera kupita ku Aroma kukafotokoza zonse kwa Kaisara. Paulo ndi andende ena anayenda pa bwato. Kunali namondwe. Andende anataya ciyembekezo ca kupulumuka.

**11 December – Kupemphera m'mabvuto**

Werengani Macitidwe a Atumwi 27.21-36

Paulo analalikira angakhale kunali namondwe. Anapemphera. Anati kuti Mulungu acita cimene alonjeza nthawi zonse. Anthu analimbikitsidwa. Cabwino coposa cimene ticite m'mabvuto ndico kupemphera ndi kudalira pa Mulungu.

**12 December – Otetezeka**

Werengani Macitidwe a Atumwi 27.37-44

Cinacitika monga Mulungu adanenera. Anthu onse anapulumuka. Anafika pa cisumbu. Adakhala m'ciopsezo cacikulu koma Mulungu anawapulumutsa. Tiri m'ciopsezo cifukwa ca uchimo. Koma Mulungu akwaniritsa ndi kufuna kupulumutsa.

**13 December – Njoka**

Werengani Macitidwe a Atumwi 28.1-6

Paulo ndi andende anali pa cisumbu cocedwa Melita. Paulo analumidwa ndi njoka. Anthu anaganiza kuti iye adzafa. Paulo sanafe. Mulungu anamusamalira. Ico cinapatsa mpata kwa Paulo kuti alalikire za Mulungu.

**14 December – Paulo ku Roma**

Werengani Macitidwe a Atumwi 28.16 ndi 28.23-29

Paulo anafika ku Roma. Analoledwa kukhala m'nyumba m'mene angalandire alendo. Anawaphunzitsa za Yesu. Anati kuti Yesu ndiye Mpulumutsi wolonjezedwa. Kodi kutanthauza ciani kwa inu kuti Yesu ndiye Mpulumutsi?

**15 December – Paulo analandira anthu ambiri**

Werengani Macitidwe a Atumwi 28.30-31

Paulo analandira anthu ambiri angakhale anali mdende. Analemba kalata polangiza Akristu okhala ku malo ena. Makalatawa apezeka m'Baibulo. Kulibe wina aliyense amene angaleke nchito ya Mulungu!

# Kulemekeza Mulungu

Lemekeza Yehova, moyo wanga – Psalm 104.1a



**16 December – Kuitanidwa kulemekeza Mulungu**

Werengani Salimo 104.1-4

M'Salimo 104 tawerenga za cilengedwe ca Mulungu. Mulungu analenga zonse zimene zioneka, monga mitengo, madzi, dzuwa ndi nyama. Poona cilengedwe ca Mulungu tingaone kuti Mulungu ndiye wamkulu.

Sabata ino tidzawerenga ndime za m'Salimo 104 pa tsiku lirilonse. Tidzaona kuti Mulungu ndiye wamkulu ndithu. M'ndime zimene tawerenga lero tawerenga zifukwa zosiyanasiyana za kunena kuti Mulungu ndiye wamkulu. Mulungu analenga zonse. Analenga dziko lapansi kuti tikhalemo. Amalamulira zonse. Mulungu ndiye Mfumu. Tizilemekeza Mulungu.

**Funso: Kodi muona bwanji ukulu wa Mulungu m'cilengedwe?**

**17 December – Cisamaliro ca Mulungu**

Werengani Salimo 104.5-9

Mulungu anapatsa madzi malo okhalapo. Anapanga mtunda kuti anthu akhalepo. Atipatsa malo okhalako. Mulungu amasamalira.

**18 December – Madzi ndi cakudya**

Werengani Salimo 104.10-18

Mulungu amapatsa madzi ndi cakudya kwa nyama ndi anthu. Cakudya ndi zakumwa ndizo mphatso ya Mulungu kwa ife. Tiyenera kumuyamikira pa mphatso zake. Kodi mumayamikira Mulungu potipatsa cakudya ndi madzi?

**19 December – Usana ndi usiku**

Werengani Salimo 104.19-23

Masiku onse dzuwa limawala. Mulungu atipatsa kuunika kuti tigwire nchito kukapeza cakudya. Usiku atipatsa kupuma.

**20 December – Nyama**

Werengani Salimo 104.24-26

Mulungu amasamaliranso nyama zokhala m'madzi. Sitidziwa nyama zonse zokhalamo. Sitidziwa kuti akhalabe bwanji ndi moyo. Mulungu adziwa. Anazilenga. Analenga zonse m'nzeru.

**21 December – Kudalira pa Mulungu**

Werengani Salimo 104.27-30

Zonse zimadalira pa Mulungu. Tifunika mphatso za cakudya, madzi ndi umoyo zocokera kwa Mulungu. Zonse ndi anthu onse afunika cisamaliro ndi citetezo cake kukhalabe ndi moyo.

**22 December – Kuganizira za Mulungu**

Werengani Salimo 104.31-35

Tiri ndi zifukwa zambiri za kulemekeza Mulungu. Kuli zambiri zimene sitimvetsa. Koma Mulungu amvetsa. Tiyenera kukondwera pa cilengedwe cake. Anthu amene akana kubvomereza Mulungu adzacotsedwa.

# Mulungu adziwa zonse

Munandisanthula, Yehova, nimundidziwa – Salimo 139.1

**23 December – Mulungu adziwa zonse**

<u>Werengani Salimo 139.1-6</u>

Salimo 139 linalembedwa ndi mfumu Davide. Davide analemekeza Mulungu pakuti Mulungu adziwa zonse.

Mulungu adziwa anthu alionse. Adziwa zimene ticita. Adziwa ngati tikhala kapena kuima. Adziwa zimene tiganiza. Adziwa ngati takondwera kapena tamva cisoni. Adziwa zimene tidzanena, ngakhale tisanalankhule. Adziwa zimene anthu ena sadziwa. Atidziwadi. Sitikwaniritsa kumubisa kalikonse.

Ndi codabwitsa kuti Mulungu adziwa zonse. Mfumu Davide anakondwera kaamba ka ico.

**Funso: Kodi kutanthauza ciani kwa inu kuti Mulungu akudziwani ndithu?**



**24 December – Mulungu ali paliponse**

Salimo 139.7-12

Mulungu ali ponseponse. Akhalako nthawi zonse: usana ndi usiku wonse. Ndi codabwitsa kuti Mulungu ali ponseponse.

**25 December – Mulungu anatilenga**

Werengani Salimo 139.15 ndi 16

Ife tonse tinalengedwa ndi Mulungu. Mulungu ana-tiona tisanabadwe. Kulibe kalikonse komwe Mulungu saona. Ndi codabwitsa kuti Mulungu anatilenga. Mulungu adziwa zimene tifunika. Tifunika Yesu. Tima-kumbukira kubadwa kwa Yesu pa tsiku la Khisimisi.

**26 December – Kuganizira za Mulungu**

Werengani Salimo Psalm 139.17 ndi 18

Mulungu ndiye wamkulu kwambiri. Sitikwaniritsa kumvetsetsa Iye. Mfumu Davide anakonda kuganizira za Mulungu. Kodi mukonda kuganizira za Mulungu?

**27 December – Kupempha thandizo**

Werengani Salimo 139.19 ndi 20

Mulungu aona zonse ndipo ali ponseponse. Cifukwa ca ici ndi Mulungu yekha amene akwaniritsa kutithandiza. Tikabvutika tiyenera kupemphera kwa Iye.

**28 December – Kukhala moyo kwa Mulungu**

Werengani Salimo 139.21 ndi 22

Mfumu Davide anafuna kuti anthu onse azimvera Mulungu. Onse ayenera kucita kufuna kwa Mulungu. Mfumu Davide anafuna kukhala moyo wake kwa Mulungu yekha. Ndi ciani cimene ciri cofunikira coposa m’umoyo wanu?

**29 December – Kupempha thandizo locuruka**

Werengani Salimo 139.23 ndi 24

Mfumu Davide anadziwa kuti nthawi zambiri analephera kucita kufuna kwa Mulungu. Anapempha Mulungu kumuthandiza. Anafunsa Mulungu kuti aone ngati kuli coipa m’umoyo wake. Anapempha Mulungu kumuonetsa cabwino. Anafunika Mulungu.

# Tsogolo lathu

Yesu Kristu ali yemweyo dzulo, ndi lero, ndi ku nthawi zonse – Ahebri 13.8

**30 December – Zonse zidzatha**

Werengain Salimo 102.25 ndi 26

Tiri pafupi kutsiriza za caka cino. Mwina caka cino cinali cobvuta kwa inu. Kapena mwina Mulungu anakupatsani zambiri zokondweretsa. Zambiri zinacitika. Zambiri zinasinthika.

Baibulo likamba kuti zonse ziri kusinthika. Cilengedwe ciri kutha. Anthu ambiri anabadwa caka cino. Ambiri anafa. Kulibe ciriconse cimene cimakhala cimodzi-modzi. Kwa ife tsogolo ndi losadziwika.

Mulungu ndiye Mulungu wa Kumwamba ndi dziko lapansi. Ngakhale zambiri zingacitike, Iye sadzasanduka.

**Funso: Kodi mukumva bwanji za tsogolo?**


**31 December – Mulungu ali cimodzi-modzi**

Werengani Salimo 102.27 ndi 28

Zonse ziri kutha. Wosasintha ndiye Mulungu yemwe yekha. Sasanduka. Mulungu adzakhalako.

Ngati si ndinu a Mulungu simutetezeka m'umoyo wanu. Mukafa kopanda Mulungu mudzakhala ku Gehena kopanda Iye. Mkwiyo wa Mulungu sudzatha. Aliyense okhala a Mulungu sayenera kudera nkhawa za kutsogolo. Mulungu adzawasamalira. Ngati ndinu mmodzi wa Iye, ndinu wotetezeka nthawi zonse. Mukafa mudzakhala naye Kumwamba kwa muyaya. Cifundo ca Mulungu sicidzatha.

**Funso: Kodi tsogolo lanu lidzakhala Kumwamba kapena ku Gehena?**



## Baibulo; Buku lofunikira kwambiri

Buku iri lidzakutsogolerani m'Baibulo ndi zowerenga za tsiku lirilonse ndi mau ofotokozera ndime za m'Baibulo. Londolani dongosolo iri:

1. Pezani nthawi yabwino ndi malo kumene kuli zii. Musalole ciriconse cokusokonazeni.
2. Pemphani Mulungu thandizo kuti mumvetsetse Baibulo.
3. Werengani ndime za m'Baibulo.
4. Werengani malongosoledwe olembedwa m'bukuli.
5. Ganizirani pa zimene mwawerenga.
6. Yamikani Mulungu pa zimene mwaphunzira. Mupempheni thandizo kuti mudzamvetsetsa zimene simunamvetsetse.
7. Citani cimene mwaphunzira.

**Werengani Baibulo ndipo mvetsetsani uthenga wa Mulungu wopatsidwa kwa inu!**

Koma Iye anati, Inde, koma odala iwo akumva Mau a Mulungu nawasunga – Luka 11.28

© Stephanos Zambia Trust.
Simuloledwa kulembanso kapena kujambula kena kalikonse kolembedwa m'buku iri popanda cilolezo.
Zithunzi ©FreeBibleimages.org with attribution to Productions International, College Press Publishing, Arabs for Christ, Richard Gunter, Good News Productions International, College Press Publishing, Rawderson Rangel and John Paul Stanley / YoPlace.com
Mukakhala ndi funso, conde musacedwe potitumira uthenga wa imelo: stephanoszambiatrust@hotmail.com.